


Nyanja

NKHANI YA
IDESI

M. M. SMITH



GREGORY.

LONGMANS' CINYANJA SERIES
THE STORY OF IDESI

Nyanja ✓


LONGMANS' CINYANA SERIES

NKHANI YA I D E S I

Buku ili linalembedwa ndi

M. M. SMITH

Jeanes School, Zomba, Nyasaland



PUBLISHED IN ASSOCIATION WITH
THE PUBLICATIONS BUREAU

LONGMANS, GREEN AND CO.
LONDON • CAPE TOWN • NEW YORK

Cinyanja : *NKHANI YA IDESI, The Story of Idesi.*

LONGMANS, GREEN AND CO., LTD.
6 & 7, CLIFFORD STREET, LONDON W.1
BOSTON HOUSE, STRAND STREET, CAPE TOWN

NEW YORK, TORONTO, BOMBAY,
CALCUTTA, MADRAS, MELBOURNE

First Published .. 1949



- Mutu
- 1.
 - 2.
 - 3.
 - 4.
 - 5.
 - 6.
 - 7.
 - 8.
 - 9.
 - 10.
 - 11.
 - 12.
 - 13.
 - 14.
 - 15.
 - 16.
 - 17.
 - 18.
 - 19.
 - 20.
 - 21.
 - 22.
 - 23.

Printed in South Africa by
Galvin & Sales Ltd., 11 Castle Street, Cape Town

CILONGOSOLO CA MKATIMO

<i>Mutu</i>	<i>Tsamba</i>
1. Unamwali wa Idesi	1
2. Banja Lao	5
3. Nyumba ya Tsopano	8
4. Mwamuna ndi Mkazace	12
5. Mwana Watsopano	16
6. Ndi Akazi Anzace	20
7. Msonkhano wa Akazi	24
8. Nyumba Yoleramo Ana	28
9. Zina za Nyumba Yoleraomo Ana	32
10. Matenda	38
11. Alendo	41
12. Kusoka Malaya	45
13. Kulemba Makalata	49
14. Mankhwala Onyenga	53
15. Sing'anga	56
16. Aceza Kwao	60
17. Zakale ndi Zatsopano	62
18. Kunyanja	65
19. Abweranso Kwao	68
20. Kumanga Nyumba	71
21. Ukwati	74
22. Ngozi	76
23. Kucipatala	79

MUTU I UNAMWALI WA IDESI



Kumudzi kwina ku-fupi ndi nyanja yaikulu kunali namwali, dzina lace Idesi, woleza mtima koma wanzeru pokhala kuti ciyambire ubwana wace anapita kusukulu.

Inde akulu ena am'-mudzimo anati kuphunzi-tsa mwana wamkazi ndi kupusa. "Nanga", ati, "Athandize mai wace ndani? Kudya azingodya wosalima. Ndani ati amkwatire wosadziwa kusinja!"

Bambo wace pomva mau amenewa anaitana amace Idesi nawafunsa kuti, "Kodi ndi zoon zimene anena anthu kuti

tampusitsa mwana wathu, kuti adziwa kudya kokha?"

Amace anakana nati, "Bodza limenelo. Idesi alibe ulesi, koma pogwira nchito agwira mwa-ngwiro namariza msanga. Akabwera kusukulu ayambira cire nchito zam'nyumba. Onani, suyu alikubwera apo ndi ufa umene wasinja lero.

Mukananena naye, popeza waika mtima wace pa nchito ya uphunzitsi. Ati mumloleze apitebe kusukulu akaphunzire nchitoyi."

Bambo wa Idesi anamuitana nati, "Katule ufawo, ubwere kuno." Mwamsanga Idesi anabvomera nabwera kukhala pansu kufupi ndi Bambo wace. Akulu aja ndikumanena ndi mwana wao kumfotokozera zimene anazona iwo eni ndi maso, pobwera Azungu pa ciyambi-yambi kumudzi kwao. Anati, "Ana a masiku ano akhumbira zacizungu zokha. Kodi Azungu asanabwere tinatani? Koma tsopano ana samvera. Ine zacizunguzi sindifuna! Ine ndinawaona alikukurukira ku nyanja, nkhope piriwiri! ndinali mwana. Akulu namadabwa kuti, 'Kodi mizukwa yanji imeneyi?' Ena anayesa kuwaletsa kuti asafike kugombe, enanso naopa nati, 'Angatilodze, mwalekeni. Koma muwapatse malo kuthengo kuja aphedwa afiti. Kumeneko ngati ali afiti akadyedwa ndi mizimu ya afiti anza?' Tangoona kuti alikumanga nyumba osafayi. Akulu anaopa nati ali ndi mankhwala amphamvu amenewa, saopa afiti.

"Kuyambira pamenepo Azungu anaphunzitsa anthu zambiri zacilendo. Anthu ena anawatsata maphunziro ao koma ine ayi. Ciyambire kale amandiyendera nayesa kundikopa ndilowe mu mpingo wao koma ndakana. Iwe ufuna kuwatsata. Cabwino, katsate, sindikuletsa. Pena akalandira mwana wanga, adzandisiya ine. Pita, mwana wanga, kaphunzire."

Ha! abambo aja sanadziwe kuti m' masiku am'tsogolo iwona adzatsata maphunziro omwe-wo, cifukwa ca mayendedwe a mwana wao Idesi.

Tsiku ndi tsiku, mwezi ndi mwezi Idesi

anapita kusukulu naphunzira zambiri. Popita zaka zitatu kunabwera Mzungu wamkulu kudzawayesa anamwali ndi anyamata kuona ngati nchito ya uphunzitsi angauthe anaona kuti Idesi wadziwa namupatsa kalata yace yonena kuti tsopano ali mphunzitsi. Pamene Idesi anayamba nchito yakuphunzitsa, makolo ace anakondwera popeza mwezi ndi mwezi anabwera ndi ndarama zace za malipiro ndi kupatsa mai wace. Kwinanso namathandiza kumunda ndi ku nyumba.

Kusukulu kumene Idesi anali kuphunzitsa kunali aphunzitsi ena amuna ndi akazi. Aphunzitsi amunawo pakumuona ndi kumati, "Eya! kamkazi kameneko! nkhope yace yokongola; kuyenda kwace kosangalatsa." Ena anafuna kuti amukwatire koma iye ndi kumati cete mpaka anafunsidwa ndi mnyamata wina, mphunzitsi mnzace amene anali wa mtima wofatsa, dzina lace Mateyu. Nkhoswe zakucimuna ndi zakucikazi zitabvomera ukwati wao anapita nakwati-tsidwa ku nyumba ya Mulungu malinga ndi malamulo a chalichi. Anauzidwa kuti ukwati umenewo uletsa mitala, kuti mkazi sangakwatire mwamuna aliyense wina, Mateyu ali moyo, nayenso Mateyu sangakwate mkazi wina aliyense, Idesi ali moyo. Ngakhale paoneke matsoka otani, sangalekane. Cifukwa Mateyu ndi Idesi anakondana kwenikweni, malangizo awa sanawabvuta, anati sangamufune munthu wina.

Idesi sanasiye nchito ya uphunzitsi koma analemba namwali kuti amusinjire, iye ali kusukulu. Mateyu ndi Idesi anasangalala ndithu, kwina analikuthandizana nchito yakuphunzitsa ndi kumaceza pamodzi za nchito zao za mitundu-mitundu. Koma anthu ena anayamba kumanena Idesi kuti, "Waulesi" ndi kumati kwa Mateyu,

"Kodi mwakwata mkazi? Munaona kuti mkazi namulekera mwamuna wace kwa mlendo, iye mwini namapita njira zace? Wonyada ameneyu! Wangodzikuza kuti 'Ine ndi mwamuna sitinasiyane', apo akakugwiritsa nchito za akazi."

Mateyu anadziwa kuti bodza limeneli pakuti Idesi akati akabwera kusukulu nayambira cire nchito za banja. Conco anawayankha anthuwo nati, "Mkazi ameneyu ndi wanga, si wanu ayi. Mungomusirira. Ngati inu muli ndi mkazi wabwino monga wangayu, muli ndi mwai. Musamunamize mkazanga, zapabanja ndi zanga zokha si zanu." Anali wanzerudi.

MUTU II BANJA LAO



Mwana wao wacisamba asanabadwe, Idesi anapita kukhala ndi mai wace, koma mwana amene anabadwa ku cipatala ca ku Mission. Anali cimwana ndithu wa mwamuna, ndipo masiku amenewa Idesi sanapite kuphunzitsa kusu-kulu. Anakhala ndi azimai akulu kumudzi naphunzira mwambo wosungitsa banja.

Cisoni ndithu, mwanayo alikuyamba kukwawa anadwala, thupi lonse kukolera moto ndi m'mimba kutseguka kwambiri. Mbuyace wa mwana anakamfunira mankhwala ndikumwetsa mwana koma kulephera kumciritisa. Anapita uku ndi uko nafuna mankhwala amitundumitundu koma zinalephereka zonse, mwana uja natsirizika.

Cisoni ndithu ! Akucimuna namanena akucikazi kuti, "Sizo ! Mwana wamkazi wanuyu watitengera tsoka ndi kuphunzira kwaceko. Amati

adziwa kulera mwana!" Nawonso akucikazi ndikumati, "Mwamunayo mayendedwe ace siti-wadziwa! Nanga mwana wathuyo wafa ninji popeza mankhwala onse analandira?" Malinga zocita zao ali, "Tiyeni ku ula."

Mateyu ndi Idesi anakana nati, "Ula sitiufuna, ula ndi bodza." Akwao nacita mantha namati, "Inu mukakana ula, adzangokunenani kuti ndinu afiti." Koma anakanabe nati, "Afiti ndani? Ife takondana, sitingaputirane milandu pa tsoka lathuli." Akuluwo nalephera namanena "Kodi! Mudzaona!"

Popita nthawi panabadwa mwana wina ku banja la Mateyu ndi Idesi, mwana uyunso ndi kudwala ndikumwalira ngati wacisamba uja. Cisoni cacikulu cinawagwera, misozi mbwe-mbwe! Akulu ali, "Sizo! Suja tinanena!" Milandu yakale aturutsanso. Amace Idesi anadandaulira mwana wace kuti, "Mwananga, msiyeni mwamunayo. Simugwirizira naye mwana." Ali pakati pa mabvuto amenewa, Dona wa ku Mission anabwera kumudzi kwao kuti akapepeze maliro. Ndipo Idesi anamufotokozera mabvuto oturukira malirowo. Koma Donayo anayankha nati, "Musakayike, ana saf-ifa cifukwa ca kunyenga kwa makolo ao, koma makamaka cifukwa ca kusadziwa kwao. Mwana akaleredwa kuli anthu amatenda, nayenso angatenge nthenda kucokera iwo." Anawauza kuti ayenera kupita ku cipatala akaonane ndi dotolo wakumeneko amene adzawafotokozera zonse.

Tsono Mateyu ndi Idesi anapita ku Mission naonana ndi dotolo. Iye anawayang'ana onse awiri nalephera kupeza nthenda m'matupi mwao. Anati aleke kudzipweteka mtima cifukwa ca zonena anthu koma maka akalambule maudzu


onse ozungulira nyumba yao ndi m'mudzi mwao kuti payere, udzudzu ndi zoipa zisacuruke. Anawapatsa kabukhu m'mene munalembedwa tsatane-tsatane masamalidwe a nyumba ndi ana, nati, "Ngati pali zina zimene simuzimva bwino, mudzandifunse, ndikuuzeni."

Mateyu ndi Idesi anathokoza dotolo nati, "Zimene mwatiuza ticita. Koma kuti tikhalebe kumudzi kwa makolo athu, iyai. Tikatero tilephera cifukwa ca iwo. Tipita kwa Mzungu woyang'a nira masukulu, akatitume ku sukulu yina yakutari, tikaphunzitseko. Ngati Mulungu atipatsa mwana winanso, akaleredwe kumeneko."

Mzunguyo anabvomera nawatumiza ku sukulu yina yakutari kuti onse awiriwo akaphunzitseko. Komweko iwo anamanga nyumba yao yeniyeni napezapo mtendere popanda ena owanena cifukwa ca kusagwiriza mwana.

MUTU III

NYUMBA YA TSOPANO



Asanayambe kumanga nyumba anasankha malo abwino pa kacitunda nati, Pano ndiponi, udzudzu sudzati-bvuta kwambiri cifukwa ndi kutari kudambo. Mwini mudzi anabvomera ndipo anamanga nyumba ya dothe lokha cifukwa sanafuna kuononga mitengo yambiri. Anaikamo mawindo kuti mupite mphepo ndi dzuwa cifukwa anaphunzira kuti pomwe pali mpweya wabwino ndi dzuwa matenda sacuruka ngati umo acuruka mundima ndi mopanda mphepo.

Nyumbayo inali ya zipinda, cipinda cina cocezeramo, cina cogonamo, cina ca alendo. Panalinsokacipinda kosungiramo cakudya ndipo kuzungulira mbali zitatatu za nyumba kunali khonde labwino. Anamanga kanyumba kophikiramo kuti pophika utsi usamafukirire m'nyumba yeniyeni. Kanyumbaka ndiko kitchini. Kutseri kwa kitchini kunali mosambira ndi nyumba

ya cimbudzi. Kufupi ndi nyumba anabzala maluwa okha natsirira madzi kuti mvula ikagwa abzalenso zina zosawirira monga ntedza ndi mbatata kapena nyemba. Zinthu zowirira zimatsekerera mphepo kunyumba ndiponso ziitanitsa udzudzu ndi njoka.

Mateyu anakonda m'nyumba mawindo ali pululu! Idesi anabvomerana naye kuti, Inde muyenera kupita mphepo yabwino m'nyumba usiku. Koma cimene cinamcititsa mantha Idesi, ndiye kuti mungalowe cirombo. Pamenepo Mateyu anakhomera nsungwi pa windo kuti cirombo cisalowe, ndipo ataona ndarama zokwanira anagula 'wire-gauze' woikapo kutinso pasapite udzudzu.

Pomanga nyumbayo ndi kukonza zonse zam'kati mwace ndi m'munda panali cinchito cacikuru. Pokhalanso Idesi anali kuphunzitsa kusukulu m'mawa uli wonse nchito inamcurukira ndithu. Koma anali wakhama napirira mpaka kumariza. Mwamuna wace nayenso anali ndi cinchito, kupanga mipando ndi matebulo ndi zinthu zina zofunika m'nyumba. Idesi sanafuna kakhala ndi katundu wambiri m'nyumba cifukwa anati, m'nyumba mukacurukamo zinthu simuseseka bwino ndipo akati aziremo, pali kanchito kuturutsa katundu yense. Anadziwa kuti akasesa ndi kupukuta m'nyumba masiku onse nazira mlungu uli wonse, napaka njereza m'makoma kawiri-kawiri, m'nyumba simukhala nsikidzi. Conco sanafuna kuti zinthu zisanjikane m'nyumba, angabvutike nazo.

Kucipinda cogonamo anaika mabedi awiri pamodzi ndi nsaru zao za udzudzu (Mosquito-nets). Kumbali kumodzi anakhoma thabwa ndi misomali yace. Pamisomalipo anapacika mauta

ndandanda kuti akolekerepo malaya ao. Inde inali nzeru yabwino pakuti popacika malaya pamauta sanakhwinyike kapena kung'ambika ndi misomali. Mateyu akati akabvula zobvala zace anapacika jeketi pauta nakolekera makabudula ace pa cingwe cace ca uta. Anakhoma thabwa lina m'munsi mwace ndiye pomwe anaika nsapato zace.

Anakhazika bokosi loikamo cuma cao panjerwa, lingadyedwe ndi ciswe, kwinsano bokosilo nayesa mpando wokhalira. M'cipinda comweco anakhoma thabwa lina pakhoma kuti aikepo zipeso za tsitsi ndi sopo ndi matswace a mano ndi lumo lometera ndebvu. Zobvala zonse ndi mabulanketi ndi zosambira anasunga m'cipinda cogonamo cokha. Kunawaipira kwambiri kuti zimenezi zisungidwe pamodzi ndi zinthu zophikira kapena zodyera nazo kapena pa malo amodzi ndi zakudya.

Cipinda cogonamo alendo anafotokozanso bwino kuti nawonso alendo apeze malo oikira ndi osungira bwino zinthu zao. Panali kacipinda kena pafupi ndi cipinda cogonamo makolo koma munalibe kanthu m'cipindamo. Anacimangira kuti akadzakhala ndi mwana wina, mwanayo angagonemo koma anayembekeza kukonza cipindaci mwanayo atamuona.

Mateyu anasamala Idesi monga mbale wace. Panali cijanano ceniceni. Pakuceza anaceza limodzi, yense pampando pace, pakudya nadyera limodzi patebulo m'cipinda cocezeramo. M'cipindaco munalitebulo ndi mipando ndi kabadi (cupboard) mosungira mbale ndi makapu, zingapitsidwe ndi ncence ndi pfumbi, cifukwa izo zitengetsa matenda. M'cipindamo munalinso mtsuko ndi madzi ophikidwa akumwa. Idesi

akaphitsa madzi mpaka atawira anaika m'mtsukomo nabvundikira cifukwa anadziwa kuti madzi am'mitsinje amaipitsidwa ndi zina zopatsa nthenda koma pophika matendawo afa ndi moto ndipo madzi ngabwino kumwa.

Patebulo Idesi anaika kamphika ndi maluwa kukometsera nyumba napacika nsengwa zopetedwa ndi mkanda zimene anapanga ali namwali. Pa mawindo anapacika nsaru zamawanga zimene anasoka iye mwini. Mateyu anamanga tsanja kufupi ndi kitchini kuti akaikepo miphika ndi mbale zipitidwe dzuwa zingasase.

Nyumba ya Idesi masiku onse inali mya! Anazira monsemo ndi m'kitchini momwe mlungu ndi mlungu. M'cimbudzinsu munali mosamalidwa, mosanunkha, mopanda ncence pakuti namonso anazira natsuka cibvundikirō cace ndikuikamo phulusa. Pakutero nchito inacuruka inde koma m'nyumba munali mokondweretsa kwambiri ndipo sanaone nchitoyi kuwawa ai.

MUTU IV

MWAMUNA NDI MKAZACE



Pokhala kuti Idesi anali kuphunzitsanso kusukulu akanalephera nchito yonsezi yam'nyumba popanda wina womuthandiza cifukwa kusukulu anakhala m'mawa wonse kuweruka usana. Apo anatenga ndarama zina za malipiro ace nalipira mbandazi amuthandize kusinja. Koma iye mwini anakonza m'nyumba nathangatanso m'munda.

Mateyu anali munthu wosamala ndipo atadzuka m'mawa anayala mabulanketi pa bedi pace ndipo Idesi alikusesa m'nyumba ndikufotokoza bedi lace, Mateyu anakoleza moto natereka madzi ometera. Madzi ali pamoto anasesa pabwalo ndi pacimbudzi. Pomwepo Mateyu alikusamba, Idesi anaphika cakudya ndipo naye atasamba, onse awiri anadya natsuka mbale ndi miphika napita kusukulu.

Amuna anzace anamuseka Mateyu nati, "Mugwiriranji nchito ya akazi? Akazi athu

alikutinena kuti sitiwathangata. Mukamacita zotere akaziwa saweruzika." Mateyu nangofunsa kuti, Kodi inu simumthangata konse mkazi wanu?

Mwamuna wina anabvomera kuti mwina inde angamuthangate koma wosati pamaso pa anthu ena. Mateyu nayankha, "Ha! ndinu wamantha, nanga manyazi ace alikuti kumuthangata mnzanu atatanganidwa ndi nchito?" Pakumva mau amenewa ndi kuona zocita Mateyu, pang'ono-pang'o no amuna ena anayamba kuthangata akazi ao mwina ndi mwina.

M'nyumba ya Idesi ncence ndi udzudzu sizinacuruka ndipo anthu ena am'mudzi atayamba nawonso kusamala nyumba zao, mudzi wonse unayamba kukongola. Nchito yina yaikulu imene anthu anacita ndiyo kukumba citsime ca madzi kuti onse amweremo. Atakumba anamanga mpanda kuti zoweta zisaipitse nakonza malo ena komwe zoweta zingamwe madzi ao.

Onse anathangatana limodzi pa nchito iyi, Nyakwawa napereka mpunga ndi mbuzi kuti anthu adye. Akazi anaphika zakudyazo anchito onse nadyapo nakondwera osadandaula za nchito.

Patapita nthawi Idesi anatenganso pathupi ndipo anati, "Ndipita ndikaonane ndi dona dotolo wa Mission akandilinge ndikundilangiza zondiyenera kucita." Dotolo wa Mission sanaonane naye Idesi kale namufunsa tsatane-tsatane za moyo wace ndi za ana aja kubadwa kwao ndi kumwalira kwao. Idesi anamulongosolera zonse wosabisa kanthu. Pamene atamulinga dotolo anamuuzza Idesi kuti wacita bwino kubwera msanga kucipatala, nati, "Patsopano m'thupi mwanu muli ndi mphamvu ndipo patapita miyezi isanu mudzabala mwana. Koma kuti mwanayo akhale wamphamvu, muzidya inu cakudya coyenera ndi cokwa-

nira. Musatope ndi nchito yolemera ndipo masiku onse muzipuma pang'ono masana."

Idesi posafuna kusiya nchito yace yakuphuzitsa, analemba namwali kumusinjira mphale ndi ufa ndi kutunga madzi ndi kuzira m'nyumba. Ali ndi miyezi isanu ndi iwiri, anayamba kusoka malaya a ncowa kuti adzambveke mwana akabadwa. Mateyu naye anapanga kabedi kace nakagula nsaru ya udzudzu yoti akamphimbire mwana. Ncembere zonse zam'mudzimo anazizwa kwambiri nati, "Kodi inu mucita ciani? Kumsokera mwana malaya asanabadwe! Kulaula kumeneko!"

Koma Idesi analibe mantha nati, "Ine mwana ndimfunitsitsa, sindingamulaule. Ndifuna kuti akabadwa papezeke zomumbveka angazizidwe ndikudwala cifuwa. Ndifuna kabedi ndidzamugonekemo ndi nsaru ya udzudzu yomutetezera ncence ndi udzudzu zingamulume ndi kumupatsa nthenda."

Pamene anapitanso kwa dotolo anauzidwa kuti, Tsopano siyani nchito ya sukulu mpaka atabadwa mwana. Masiku otsalawa uzikonzera cire nchito zonse zam'nyumba." Cakudya cimene anadya Idesi cinali cotere. M'mawa anaphika phala nasanganiza ndi mkaka wa mbuzi mwina wa ng'ombe. Masiku ena anamwanso tii (tea). Pausana anaphika nadya nsima ndi ndiwo yabwino monga nyama, nsomba, mazira, nyemba ndi masamba, madzulo comweconso. Koma sipanapite tsiku wosadya masamba ndi zipatso. Kudya kwace anadya bwino wosakhutitsa kwambiri angamve m'mimba. Dotolo anamulangiza kuti kufunika makamaka amwe madzi ambiri ndipo anaterodi. Mwina anapfanyira madzi a mandimwe m'madzimo.

Cifukwa ca khama lao m'munda sanasowe

ndiwo za masamba kapena zipatso. Anali ndi matimati, nthoci ndi mango. Analinso ndi nkhuku zoikira ndi atambala amene anapha nadya kamodzi-kamodzi. Mateyu anagula mbuzi ziwiri zazikazi kuti apeze mkaka ndipo pamene mbuzi zinauma anagula mkaka wa ng'ombe. Cakudya cimeneco cinampatsa Idesi mphamvu yabwino. Mateyu anathangata mkazace kwambiri angatope popeza dotolo anati mkazi sayenera kusenza zolemera ali ndi pathupi.



MUTU V MWANA WATSOPANO



Masiku a Idesi anamukwanira kuti abale ndipo anapita ku cipatala, ikumene analako mwana wamwamuna. Pomuyesa pa sikelo anapeza mwanayo kukula kwace anafikira pa 7 lbs.

Mateyu anali wacimwemwe ndithu natumiza mthenga wa lanya kwa apongozi ace kuti, "Mwana wanu ali ndi mwana wamwamuna. Ali moyo onse." Idesi anagona masiku kucipatala kuti akapumule tsono napita kunyumba ndi mwana nakamugoneka m'bedi

limene Mateyu anakonzera cire.

Azimai onse anabwera amuone mwana nati amuyangate koma Idesi anawapepeza kuti, "Conde mumulole agone angacenjere ndi kufuna kunyamulidwa tsiku lonse. Ine ndiri ndi nchito zambiri ndipo ndimunyamula bwanji? Kwinanso tulo tace tapabedi tidzamuthandiza kukula ndi mphamvu."

Tsiku lina mkazi wina anampeza mwanayo alikulira namufunsa amace kuti, "Kodi mwanayo simumuyamwitsa?" Idesi anayankha, "Iyai, wayamwa posacedwapa, tsopano ndimupatsa madzi ophika kuti amwere m'sipuni. Popita ora limodzi, dzuwa lirikulowa ndidzamuyamwitsanso. Mkaziyo nazizwa nati, "A! A! mwana akalira wosamuyamwitsa!" Idesi anamuza kuti nthawi zace zoyamwitsa mwana zinali:— 6 okoloko ndi 9 okoloko m'mawa, 12 okoloko masana, 3 okoloko masana, 6 okoloko madzulo ndi kamodzi kokha usiku. Kwinanso anafotokoza kuti kamodzi patsiku anapfinyira mwana madzi a zipatso, kapena lalanji kapena papaya ngakhale matimati namumwetsa masipuni awiri ang'ono nati "Akakula, ndimuonjezera". Mkaziyo anadabwa kwambiri nakakamba nkhani yonseyo kwa akazi anzace nati, "Akazi a mphunzitsi ali ngati wamisala! Kodi mwaona mwana nakula ndi kuyamwa kokha! wosadya konse! Ati koma madzi ndi madzi a zipatso! Ha! Inu!" Zocita Idesi zinali zosamveka kwa akazi enawo ozolowera miyambo yakale. Kulimba mtima kwace kuja ndi cimene cinamuletsa kubvomerana nawo akamutsutsa.

Mwina akamuseka kwambiri monga tsiku lina m'mene anzace anampezera alikukhazika mwana wakhandayo pamphika kuti akodze, mwanyo nakodzadi. Koma ena anayamba kumbvomerera poona kuti mwanayo sanaipitsa mtemwende ndipo amace sanabvutika kutsukatsuka zoipa monga amai a ana ena.

Tsiku lina bwenzi lace la Mateyu linafika kunyumba kwace nati, "Mwamnawe! Ndadula cimtengo kuphiriko, ndidzamangire nyumba yanga. Tatiyeni ndikusonyezeni." Mateyu ana-

pepeza kuti, "Ndikanapita koma ndirikuyang'ana mwana, mai wace wapita kumsika, namusiya mwana ndi ine, kuopa pfumbi ndi ncence ndi kutentha kumsikako." Mwamunayo nati, "Kodi mwanayu waleka kale kuyamwa?" Mateyu nati, "Ayi amayamwa." Munthu uja nati, "Ho!" naomba manja, "Kodi mwaona mwamuna naya-mwitsa mwana! Akalira mutani naye?"

Mateyu anaseka naye nalongosola kuti mwana wace tsopano wazolowera kuyamwa pa nthawi ndi nthawi, samalira-lira koma akati alire adzamumwetsa madzi pang'ono kudikirira kubwera kwa mace. Mace adziwa nthawi yace yoyamwitsa ndipo adzabwera pa nthawi yoyenera.

Munthuyo anati, "Kufikira lero sindinaona mwamuna akupusitsidwa ndi mkazace wosadandaula! Kodi ndinu anthu otani osaopa miyambo ya makolo? Mwanayu mumulaula." Mateyu anakana nati, "Mverani, ndikufotokozereni zandionekeera ine. Ine ndinakwata mkazi uyu ndipo anandibalira mwana. Akulu anatilangiza ndipo tinamvera malangizo ao koma mwana natifera. Ndiye ndikubadwa wina nayenso natifera. Uyu wacitatu tirikulera monga watilangiza dona doto-lo wa ku Mission. Azunguwa ali nazo nzeru zao nathandiza anthu ambiri akudwala, nane ndikhulupira kuti nzeru zao zitithandiza ife, tika-mvera bwino."

Izi munena kuti mkazi wandipusitsa, bodza limenelo. Mkazanga andikonda ndithu, sangacite kanthu kakuti andicipitse ayi. Onani lero ndi namuuzwa ndine kuti mukafuna kupita kumsika, pitani, mwana wathu ndimuyang'anira ine. Siti-funa kuti mwana asauke kumbuyo kwa mace ndi dzuwa ndi ncence ndi pfumbi. Kumsikako amapita anthu odwala zifuwa ndi maso ndi

matenda ena. Ife tifuna kuleretsa mwana wathu nthenda zonsezo." Popeza Mateyu sanathe kupita kuphiri, mnzaceyo anakhala pansi naceza, Mateyu alikupanga kampando, mwana ali m'tulobe.

Kampandoko kanali ka msinkhu woyenera mwana woimirira, kanali ndi matabwa m'mbali mwace kuti mwana asagwe. Pokhalira pace panali ciboo cacikulu kuti mwana angakhalepo nakodza. Kumunsi kwa mpando anati aike mphika wokodzeramo.

Mateyu anati kuti ana a Azungu ali nayo mipando yotere naphunzira kuti asaipitse m'nyumba. Mnzace uja analikuluka mkeka ndipo pakuti mlaza unamthera anatsazika nati, "Zikomo, mwandicezetsa. Tionananso."

Idesi pobwera madzulo kumsika anapeza mwana ali cigonere m'bedi mwace, ataphimbidwa nsaru yace ya udzudzu, ndipo anayamba kutereka ndiwo ndi nkhalu. Anamuuzza Mateyu kuti akazi anzace anamusirira kuyenda wopanda mwana, iwo ana ao alikulira ndi dzuwa. Koma ena anamunena kuti, "Wouma mtima iwe!"

MUTU VI NDI AKAZI ANZACE



Idesi anayambanso nchito yakuphunzitsa nali-pira namwali wakumuthandiza kunyumba. Mwana anamugoneka mu dengu naika pakhonde pasukulu ndipo sanabvuta konse mace ali m'sukulu. Anamuyamwitsa asanalowe sukulu, namuyamwitsanso ataturuka sukulu.

Posacedwa mwana anayamba kucenjera nafuna kukhala tsonga ndi kusewera. Mace anamutsamila pa pilo (pillow) nampatsa mikwijnjiri kusewera nayo. Anasokanso cinyao cansaru cofaniza kagaru nacitsendera ndi thonje mwana nasewera ndicinso.

Mwana anayamba kukhala tsonga ali ngati miyezi isanu ndi iwiri ndipo dotolo anamuuza Idesi kuti tsopano ayambe kumuzoloweretsa cakudya cina. Conco anamuphikira kaphala ndi mkaka namudyetsa pang'ono kamodzi patsiku, atayamwa kale. Pokulanso pang'ono ndi kuturuka

mano anayamba kumpatsa msuzi wa ndiwo, masamba ndi mazira ndi mbatata pang'ono zomenyedwa bwino mu sefa. Dotolo anamulangiza maperekedwe ace.

Kamwanako kanali kamphamvu ndithu, koseka-seka. Dzina lace anamuca NDALA. Akumudzi ena anazizwa kuti sanampatsa dzina la Cizungu popeza makolo ace anatsata miyambo yambiri ya Azungu. Koma Idesi analongosola nati, "Inde zacizungu zambiri ziri zabwino zothangata moyo wathu koma kulibe phindu ndi dzina lokha lacizungu. Mwini wako likakukonda dzinalo ndi momwemo basi! Tisangoti zonse zacizungu nzabwino, zonse za makolo athu nzoipa koma tisankhe ziri zonse zabwino."

Mcembere wina anayankha nati, "Inde nzoona koma m'kusadziwa kwathu timangoti nzabwino zonse. Adzatiuza ndani kuti koma sankhani cakuti? Anakuphunzitsani inu zacizunguzi ndani?" Idesi anawauza kuti ku Mission kuli dona wokoma mtima, wodziwa za mankhwala ndi za kulera mwana, yemweyo ndiye anamulangiza. Akazi anzace anati zikanakhala zabwino nawonso akanaphunzira kwa iye cifukwa mcebere acita manyazi kupita kusukulu pamodzi ndi ana. Ndiponso zophunzira ana ndi zina, zoyenera kudziwa mcebere ndi zinsano. Iwo amafuna kudziwa masungidwe abwino a nyumba ndi banja.

Anati, "Kodi dona mukumuculayo sangati-komere mtima ifenso ndi kudzatiphunzitsa? Kapena alira ndarama zambiri asanabyomere." Idesi anayankha nati, "Zandaramazo iyai, safunsa ndarama, maka afunitsa kutumikira anthu kuti nawonso akonde Mulungu ndi anthu anzao. Ndidzamufunsa donayo ngati nkutheka abwere kuno kukuphunzitsani."

Comweco tsiku lina anakamuona dona dotolo wa ku Mission namuuzza zimene apempha akazi anzace. Dotolo anakondwera kumva za akazi ena ofuna kuphunzira kusunga banja ndi kulera ana ao bwino nati afuna kuwathandiza koma kuti kuyenda ku mudzi kwao kutenga nthawi. Kucipatala kunali odwala ndipo sanathe kuwalekerera tsiku lathunthu iye alikuyendera kumudzi kwa akaziwo. Anati, "Ine ndiri ndi galimoto, koma kulibe mseu kumudzi kwanu kopita galimoto. Bwenzi ndikanabwera ndi galimoto nditaperekerera mankhwala ku cipatala m'mawa ndi kubweranso usana kuti ndionane nawo odwala ocurukawo. Citi cindiletse ndi mseuwo."

Idesi anabvomera nati awauza akazi anzace mau ace a Dotolo. Dotolo anamuonetsa Idesi kamwana kakhanda kamene kanabadwa kucipatala nthawi isanakwane. Kanali kakang'ono-ng'ono, kofooka ndithu, kankhope kukula kwace ngati dzira la bakha. Kanali gone m'kabedi maso pheti! Mbuyace wa kamwanako anada nkhaba namakhala pafupi kumuyang'anira, nkhope dwi! Analibe mdzuku ndipo anaika mtima wace pa mwanayu. Amadandaula kuti, Kodi mwanayo angacire popanda mankhwala? Cibadwire sanamwe mankhwala koma amangomupfanyira maere a mace. Si kulaula kumeneko! Ati munaona akupfanyira maere m'kapu! Ucisi! Ndipo pamene amati amufunire mankhwala akumudzi amusambitse, amukaniza. Kumeneko nkutani? Cibadwire mwana sanasambe ndi madzi omwe sanasambe nawo! Dona dotolo ati, "Kusambitsa ayi koma timudzole mafuta otentha basi!" Izi nzimene amadandaula mbuyace mwana. Dotolo anamuuzza Idesi kuti mwanayo akapitidwa mphepo azizidwa ndikumwalira ndico cifukwa

cace samusambitsa. Ndiponso kanalibe mphamvu yakuyamwa conco amupfnyira maere amace ndi-kumudyetsa, kangafe ndi njala.

Dotolo atapita kuona ena odwala, Idesi anaceza ndi ambuye wa mwanayo kuyesa kuwatozozza mtima. Anawaonetsa mwana wace Ndala nati kuti mwanayo analeredwa malinga ndi malangizo a dotolo ndipo suyu cimwana ndithu! Anati, "Musaope kuti mwana wanu adzamulaula ayi. Kodi kumudzi mwana wotere angacire ngati? Koma onani, wanuyu wakhala masiku ndipo thupi lace lioneka kuti likubwera."

Akuluwo anabvomera koma anatunthumira kuopa mkwiyo wa mizimu popeza sanamvera miyambo ya kale ya makolo. Idesi anati, "Makolo athu anali anthu anzeru natsiyira nzeru zao m'miyambo yao. Pano apita ku malo a mizimu. Kodi kumeneko ife tidziwa bwanji zolingirira zao? Pena amationa ife nati, "Ha! ana athu kupusa! Saphunzira zatsopano, angodya mkute wa dzulo basi, nyama yalero osaiphika? Pena mizimu itiyesa opusa pokana zabwino zatsopano." Akuluwo anabvomera nati adzamvera malamulo a dotolo kuti mwana aciritsidwe. Idesi anabwerera kwao nakondwera kuti anathangata akuluwo ndi dotolo yemwe.

MUTU VII MSONKHANO WA AKAZI



Idesi atafika kwao pamadzulo anasonkhanitsa akazi onse kuti amve mau a dona dotolo. Anati, "Mau anu aja ndinawauza adotolo ndipo anakondwera kumva kuti munafuna kuphunzira. Anati akanabweradi kudzatiphunzitsa koma cifukwaca kutalika kwace sangayende pansipakuti kucipatala kuli anthu ambiri akudwala ndipo sangawasiye tsiku lonse osawayendera. Inde mwana wa Mariya amamuthandiza kucipatala koma iye angopereka mankhwala malinga ndi lamulo la dotolo ndipo popanda kulangizidwa sangapereke. Conco adotolo ayenera kuyendera odwala kawiri-kawiri.

Pamenepo mkazi wina anatsutsa nati, "Nanga apo tinamuona dotolo alikupita mu galimoto kuyendera midzi yina. Alekeranji kutiyendera ifenso?" Koma Idesi anayankha kuti mseu

wao waipa kwambiri ndiponso pa mtsinje panalibe mlato. "Pakanakhala mlato ndipo mseu akaulima bwino bwenzi dotolo akanafika kunonso."

Mkazi wa nyakwawa anauka nati, "Amai, zoonza zimenezi, mseu ufunikadi. Tiyeni tinene nawo amuna athu. Akazi onse anabvomera nabalalika ku nyumba zao. M'mawa mwace kunafika mthenga kunyumba kwa Mateyu kuti kuli msonkhano wa amuna pamadzulo kukamba za malimidwe a mseu ndi mamangidwe a mlato. Atasonkhana onse anabvomera kuti nchitoyo njofunikadi nati akazi ndi ana akulu azilambula maudzu a mseu, anyamata adzaze ndi miyala maenje ndi m'mene munakumbika m'mseu ndipo amuna akulu amange mlato. Nchito inagundikadi ena kulima, ena kututa miyala ndi mitengo. Atatanda mitengoyo ena anapita ku Mission kukatenga matabwa ndi misomali. Matabwa anakhoma pamwamba pamitengo, posacedwa mlato numangidwa wabwino ndi wolimba.

Anthu onse anakondwera poona mseu ndi mlato, eni njinga cifukwa mokumbika ndi mowirira munakonzedwa, ndi ena cifukwa sanabvutika pooloka mtsinje ndipo sadzatsekeredwa pa nyengo ya mvula. Zonse zitatha bwino anatumiza mthenga kwa dotolo, ndipo anayankha kuti abwera m'mawa mwace mu galimoto. Tsono m'mawa mwace akazi onse anasonkhana kubwalo, amunanso anafika kudzanso ana kuti adzaone ziti zicitikeko. Pofika dona dotolo ana anamlambira ndi nyimbo yao, ndipo anyakwawa ananena mau olonjera nati, "Akazi athu aphunziradi zinthu zambiri koma zina zawaperewera. Apo tikondwera kweni kweni kuti ambuyathu atiturukira kuti adzaphunzitse ana ace. Tiyang'anira inu, kulibe wina amene tingayang'anire.

Onani, takulimirani mseu, takumangirani mlato. Tati amai asabvutike kuyenda pansu." Akuluwo ananena mau ambiri otere, ena osyasyalika, ena oona akumtima.

Dotolo anathokoza anthu cifukwa ca mau ao nawatamanda cifukwa ca nchito yao yomuthandiza ndi cifukwa analikukometsera ndithu mudzi wao. Anati asayembekeze kuti iye mwini ndiye adzaweza moyo wao. Iye angolozza njira, koma akafuna kuturukira moyo wabwino, ayende m'njiramo iwo eni. Iye sangathe kuwalamula zimene awaphunzitsa, iwo okha mwa kufuna kwao angacite. Akafuna midzi yokoma ndi mabanja a moyo wabwino, ayenera kuthangatirana wina ndi mnzace. Atatha kunena ana anapita kusukulu, amuna ku nchito zao ndipo iye anayamba kuphunzitsa akazi.

Tsiku lina anaphunzitsa cakuti, tsiku lina cina sinthane-sinthane. Mwina anayesa ana ang'ono pasikelo kuona kukula kwao, nayang'ana matupi ao kuona ngati analikukula ndi mphamvu. Mwina anaonana ndi akazi a pathupi kuti awalangize za masamalidwe a moyo wao kuti abale ana amphamvu. Anawaphunzitsa zakusamala m'nyumba kuti musaipemo makamaka iwo amene anayamba kumanga nyumba zatsopano ndi kukamo zipangizo zina ndi zina zokometsera nyumba.

Tsiku lina anapita nawo akazi ku munda wakudimba nawalangiza za ndiwo ya masamba ndi mbeu zina ndi umo zithangata ana moyo wao. Maphunzirowo anawakomera akazi koma anada nkawa pakumva bingu la mvula, nati, "Kodi maphunziro athu tidzacita bwanji mvulayi ikagwa? Tiyeni timange sukulu yathu." Conco anakapangana ndi amuna, nayamba kumanga nyumba. Anazika misici namangirirapo ncha-

namira ndi nsungwi nafolera maudzu. Kumbali kodzera mvula anamangapo tsekera kuti mvula isalowemo. Akazi anatenga mitengo ndi maudzu, amuna namanga nyumba. Nyumba yoyambayo inali ngati msasa cifukwa cakufulumiza pakuti mvula inali pafupi. Anati amange nyumba yabwino yolimba caka camawa.

Pakudza mvula nchito yakumunda inacuruka ndipo akazi anasonkhana kawiri kokha pa mlungu.

MUTU VIII

NYUMBA YOLERAMO ANA



Idesi anali ndi cinchito ndithu tsopano, nchito yapabanja, nchito yakusukulu ndi miso-nkhano ya akazi. Mwana wace naye analiku-kwawa ndipo sanathe kumusiya payekha mudengu. Maka pa nyengo ya mvula mace anasowa kumene angamuike asewere, iye mwini ali kusukulu. Akazi ena analikudandaula zomwezo.

Tsiku lina Amanansi, mkazi wa nyakwawa anasiya mwana wace ali m'tulo m'nyumba, iye napita kukacera ndiwo. Mwanayo anauka mace kulibe ndipo pobwera anampeza mwana aliku-kwawira kumoto. Kusati mace anabwera msanga bwenzi mwanayo atapsya moto.

Idesi sanafuna kubereka Ndala kumbuyo popita kumunda pakuti anaphunzira kuti mwana akazizidwa mvula kapena nsaru zace zikanyowa, angayambe cifuwa, cimfine kapena cisoma. Koma anaopa kumusiya ndi mkazi amene analikutha-ndiza kunyumba cifukwa angamusiye kanthawi,

ndipo mwanayo angasimbwe. Conco pamene dotolo anafikanso anamufunsa kuti acite ciani. Dotolo anawasonyeza zithunzithunzi za ana a Azungu alikudya pamodzi ndikugona pamodzi ndikusewera limodzi kusukulu. Anawauza kuti ku England kuli masukulu ambiri otere a ana ang'onong'ono. Maka ndi nyumba ndi bwalo mosungira ana ang'ono, amai ao ali kunchito.

Amanansi anasirira ndithu sukulu yotere nati, Azungu inu mwadala. Nanga ife osauka titani? Kungobereka kumbuyo basi! Mkazi wina anabvomerezapo koma iye anati mwana wace amakana kumbuyo cifukwa wazolowera kugona payekha m'dengu.

Dotolo nayenso anabvomera zonena akazi nati iyenso anabvutika nawo ana kusokosa pamene akazi analikuphunzira pa misonkhano, kwinsano sanathe kumva bwino maphunziro cifukwa ca kuyendayenda kunja ndi ana oliralira. Dotolo anati, "Bwanji timange malo athu kuno kuti ana asamalidwemo, inu muli kumunda kapena kumsonkhano?" Feria, mkazi wa mmisiri wina anati, Ana sangalole, acita mantha kukhala kulibe amai, alira ndi njala. Dotolo anati ana onse anaona ku masukulu otere ku England anali osangalala nati, "Ana anunso adzasangalala akasewera pamodzi m'malo mwa kungoberekedwa kumbuyo."

Mkazi wa nyakwawa anati, "Nanga tipeze kuti sukulu yotere pokhala ndife osowa?" Dotolo nafunsa, "Kodi mlatowo munalipira ndarama zingati?" akazi nati, "Ayi, tinacita tokha." Kumannga nyumba ya ana tingamange, koma ndani ati ayang'anire anawo?" Pakumva mau amenewo akazi onse anayamba kunena wina zace, wina zace kuyesa kupeza poturukirapo.

Ena anati, Tisonkhetse ndaramo zolipira mleri, koma ena anakana kuti ndarama sizing'aneke, zibvuta. Pamenepo Idesi anati, "Mverani ananga, bwanji ife eni ana tizilandizana kuwalera ana. Pokhala ndife ambiri sizingabvute. Ena ali kumunda kapena kusinja kapena kumsonkhano, awiri tirikulera ana. M'mawa mwace ena nawalandira anza. Masiku oyamba ana azileredwa kunyumba ya ana kum'mawa kokha, masana aleredwe ndi amai ao."


Akazi anabvomera kuti zingatheke akapanzana kutero. Mcembere wina anawakumbutsa kuti nkhaniyo iyenera kupita kwa amuna pakuti akazi paokha sangaithe nyumba kuimanga. Amuna anakomana ndi dotolo kuti amfunisitse nzeru izi zakulera pamodzi ana akhanda ku nyumba yaoyao, amai ali kumsonkhano. Azibambo ena anatsutsa nati, Akazi alero ulesi! Kodi kulera ana si ndiyo nchito ya mcembere? Kodi mace mwana azingoyenda ngati namwali? Dotolo anabvomera kuti, Inde kulera mwana ndi nchito ya mace, koma mwina mwana amasauka poberekedwa kumbuyo kapena pokhala pansipafupi ndi moto mace alikugwira nchito za banja. Akazi akalandizana kulera ana, bwenzi ana akupeza malo abwino ogona ndi osewera, amai nawonso napeza danga logwira nchito mosabvutika ndi ana olira.

Bwino lace amuna onse anabvomera kuti athandize kumanga cimsasa coyenera ndi mpanda wozungulira bwalo la masewera. Akazi nawalonjera ndi kuomba m'manja nati zikomo. Msonkhanowo pobalalika, kunamveka wina akuti, "Amuna amakayika kuti khaya zitheka. Tiyeni tizilimbike nchitoyi, angatiseke." Nyakwawa ana-pfuulira akazi nati, "He! tikakumangirani nyu-

mbayi,
Akazi n
timakun
ngirani
nezi?"

MUTU IX

ZINA ZA NYUMBA YOLERAOMO ANA



Anthu onse paku-thandizana sanakhalire kumanga nyumba yoleraomo ana, ndipo zonse zitakonzeka akazi awiri anasankhidwa oyang'anira ana tsiku lakuyamba. Pokhala kuti zinali zacilendo Idesi anabweranso kuti awathandize.

Zoona ana anali amantha pamene amai anawasiya, nawonso amai anakayika mtima pakuganiza za kusiya ana ao alikulira. Koma anazizwa popeza kuti ana ambiri anatontozeka msanga, Idesi ndi akazi ena awiriwo atanena

nawo mofatsa ndi kuwagawira zosewera nazo zimene akulu anawakonzero cire. Kamwana kena kamkazi kanatontozedwa ndi kamtondo ndi kamunsi nayamba kusinja mcenga, ali phe! Ana ena anatolatola nasewera nawo matabwa ndi timabokosi ndi timagareta. Ena anali ndi timakasu ta thabwa, timipando ndi timatebulo.

Mwana wina anali zende pa katungwi, alikusekerera. Komabe ana ena owerengeka anali dwi paokha misozi mbwe! Idesi anawaitana pamodzi nawayimbira nyimbo. Posacedwa ana nawonso analikuomba manja ndikuyimba mabvume ace, ena namabvina. Tsopano misozi palibe onse ali osangalala. Idesi anawaphunzitsa masewera amitundu-mitundu, kulumphacingwe, kuponya mpira, kuumba ana adothe ndikuwabveka zigamba zotola kukhonde kwa atelara.

Ana akhanda anali gone ndandanda m'madengu a fodya atapfunda mabulanketi. Ena anali m'tulo, ena namadya zala zao kapena kusewera ndi mikwinjiro. Okwawa ndi oyamba kuima monga a msinkhu wa Ndala analikusewera pamphasa ndi zipangizo zina za zigamba zimene amai ao anasoka kusukulu. Zigamba zina anadula kufaniza ana, zina kufaniza agaru, amphaka, apusi, abakha ndi zinyama zina. Amai atazisoka anazitsendeza thonje kapena makoko a cimanga oduladula bwino. Izi zinakondweretsa ana okwawa, koma kunali zina zamitundu-mitundu zosewera nazo ana akhanda.

Mwina m'kati mwa bwalo munali mpanda ndipo kutseri kwa mpanda anaika miphika ya ana. Popita nthawi pang'ono, Idesi anatuma ana kumeneko kuti azolowere kupita kucimbudzi m'malo mwa kuipitsa malaya ndi pabwalo. Cizolowezi cimenezi cinali cobvuta pang'ono, koma malinga ndi kupirira kwa akazi olera ana cinatheka m'tsogolo ndipo cingabute kuwazoloweza komabe kubvutako kunali ndi phindu lenileni pakuti ana analeka kuipitsa mphasa ndi munyumba popita kwao.

Dzuwa litakwera pang'ono mkazi wothandiza

Idesi anabwera nawo mphika waukulu wodzala phala. Phalalo anapanga mitama ndi mkaka. Pokhala mkaka wa ng'ombe unasowa anapanga mkaka wa soya. Kupanga mkaka wa soya anaterere :— Usiku ananyika soya m'madzi, m'mawa mwace anazimenya kucotsa makoko. Tsono anasinja mumtondo ngati mtendero, natenga kapu nadzaza ndi msinjiro wa soya natsantula m'mphika. Kapu yomweyo anadzaza kawiri ndi madzi nasanganiza ndi msinjiro, comweco mpaka kumariza soya yonse, kapu imodzi soya, makapu awiri madzi. Atatakasa anaphika pamoto mpaka kuwira panthawi pang'ono, tsono nasuza mu kape. Msuzi wacewo ndiwo mkaka wa soya. Mkakawo anaphika nawo phala ndi mitama kapena mpunga.

Phala litapola ana anasamba m'manja nakhala ndandanda pamphasa. Amai anawagawira yense mbale ya dothi yodzala, phala ndi supuni yathabwa yodyera nayo. Mbale ndi supuni zinapangidwa ndi makolo a ana. Ana ang'ono olephera kudya okha anadyetsedwa ndipo amai a ana a khanda anasiya nchito zao kapena kuphunzira kwao nabwera nayamwitsa ana ao. Masiku oyamba anabwera monthunthumira kunyamula ana ao ndi kufunsa ngati analira kwambiri. Pakumva kuti sanabvuta kwambiri mitima yao inakhazikika.

Ana atamariza kudya, anapita kukodza ndipo atasambanso m'manja ndikutsangula pakamwa, anawagoneka. Ana a misinkhu yokwawa, ndi ena ongoyamba kuyenda ndiwo makamaka osowa kupuma. Ana otero sakhalira kutopa ndipo akatopa alira. Ana othamanga anawakhalitsa pamphasa munyumba. Ena a iwo anasewera ndi dothi loumbira mphika naumbira zao za masanje. Ena anamanga nyumba ndi matabwa,

enanso natunga mikanda yaikulu ya gobede kapena ya matabwa.

Akazi atamariza nchito zao anadzatenga ana ao. Mwina poona amai ao anayamba kulira, amai naganiza kuti analikulira conco ciyambire m'mawa. Koma anthu opita m'njira anati, "Iyai kulirako anangoyamba, atakuonani inu." Posacedwa ana anazolowera kubwaloko, masewerowo nawakonda kotero kuti mwina amai akabwera sanafuna kupita kwao. Tsopano nyakwawa anati, "Tiyeni tiike malamulo oyenera bwalo la ana, pangaoneke wina wotsutsana ndi mnzace." Atanena nawo Mateyu ndi Idesi anaika malamulo awa :—

1. Amai onse alandizane kulera ana kubwalo. Tsiku ndi tsiku pasankhidwe amai awiri oyang'anira pabwalo ndi olera ana pa tsiku limodzi, m'mawa mwace awalandize amai ena awiri ndi comweco tsatane-tsatane. Akapeza kuti ana awacurukira amai awiriwo, asankhe wacitatu wothandiza.

2. Atate ali yense apange cosewera naco mwana ndipo pakuti ana sakhalira kuswa zinthu, acipange colimba. Patapita miyezi iwiri apange cina. Zipangizozo azitule kwa nyakwawa amene adzapereka kubwaloko.

3. Anyakwawa adzasonkhanitsa makolo a ana nthawi ndi nthawi apangane zakufotokoza nyumba ya ana, ingagumuke kapena kubvumbwa mvula.

4. Mai ali yense pa tsiku lolemba mlungu uli wonse abwere ndi muyeso wa soya ndi muyeso wa mitama kapena mpunga kuti pakwanire cakyadya codyetsa ana kumpanda. Amai oyang'anira kubwalo asanawerukeko anyike soya m'madzi kuti anzao pobwera m'mawa azipeze zitafewa.

5. Mwana ali yense wodwala asafike ku bwalo la ana. Mwana akabwera ali bwino, matenda namaturukira ali kubwalo, amai olera amugoneke pa yekha, atumize mau kwa amace adzamatenge kupita naye kwao kapena kucipatala.

Paciyambi amai ena anaganiza kuti malamulowo ngobvuta nati akaleke nchito ya bwalo, koma posacedwa zonsezo zinawakomera cifukwa anapeza ana alikusangalala ndipo iwo eni anatha kukagwira nchito zao osabvutika ndi kubereka ana tsiku lonse. Nawonso ana anaphunzira zambiri ndi kuyamba kucenjera. Ana ang'ono ayenera kuphunzira kucita okha zinthu zambiri. Kubwaloko anawapatsa mabokosi kuti posewera azikwekweretse kulimbitsa manja. Zosewera zina zinali zolemera pang'ono monga matabwa omangira tinyumba tamasanje. Pothamanga uku ndi uko ndi kukwera pamwamba pa makwerero ang'ono, analimbitsa miyendo yao naphunzira kusagwa.


Akulu anathangata amai kupereka soya. Anandandalitsa mbale ndi masupuni odyera phala, ndipo cakudya citatha, anathandiza kutsuka mbale. Amai ena anazizwa kuona kuti mwana anakana kusewera ndi cinthu cimodzi tsiku lonse koma Idesi anawauza kuti ndiwo makhalidwe a mwana kutero, sakhalitsa pa kanthu kali konse kangakhale kokoma, akonda kusintha-sintha. Mwina ayenera kuthamanga-thamanga, mwina kusewera yense payekha cetecete, mwina kupeza danga lopumula m'tulo pausana. Aziloledwa kusankha okha cosewera cimene ciwakonda. Akatopa naco asamulole kungocitaya pansi iyai, akacibweze ku malo ace kukabadi.

Comweco tsiku ndi tsiku ana anaphunzira kusamala zinthu, naphunziranso ukhonkho ndi

ulemu n
Amai nav
a ana.

ulemu ndi kuthandizana ndi kumvera akulu. Amai nawonso anaphunzira zambiri za maleredwe a ana.

MURU X
MATEMBA



Patena amaka jamba lakini ana odwala
zangira ku bwalo jama nako anandikwa kuni
ndi coopwa kufi wothwa nawero ndi wamoyo
Chawa pakuliro yalanda ana anandikwa kwa
ana anayo. Koma muna n'edwala ngiti aye
muna kucitola. Pando xia ngi n'edwala
xamala kumala; anho odwala anayandana.
Tali na ana oyo na kawa la ana
anano kadhala kama ana la k'kondo la d'wi!
pachka wawawira. Pambona anawaka ak'ka
dwa coo ana la anawawira. Pambona
pachka anawira ana kava muna kufi.
"Anawawira ngwa ana ak'kondo." Muna
Akanda anawawira ngwa ana kava muna
ngwawira. Doko ana anawira odwala muna
koma kuni n'edwala la anawira ana ana ana
ndi k'kondo anawira la koma kuni ngwawira
ndi anawira. Anji, Mawawira ngwa k'kondo
ngwa.

MUTU X MATENDA



Pamene anaika lamulo lakuti ana odwala asapite ku bwalo laana, makolo anauzidwa kuti ndi coopsya kuti wodwala asewere ndi wamoyo cifukwa pakutero matenda ena apititsidwa kwa ana amoyo. Koma mwana akadwala apite naye msanga kucipatala. Nthenda zina ngati nthomba zimafala kwambiri, anthu odwala akayenderana.

Tsiku lina amai oyang'anira kubwalo la ana anaona kabuthu kena, dzina lace Nkondei ali dwi! payekha, wosasewera. Pomuona anaoneka alikudwala, conco amai aja anamugoneka pamphasa payekha natumiza mau kwa mace mwana kuti, "Dzamtengeni mwana wanu alikudwala." Mace Nkondei anabwera msanga napita naye mwana kucipatala. Dotolo anati mwana adwala malungo koma kuti nthenda iyi sipitirira kwa anthu ena ndi kukhala pamodzi ai koma pokha polumidwa ndi udzudzu. Anati, Mwacita bwino kubwera naye.

Tsiku lina Idesi anamva ana a ku mudzi wina wapafupi anadwala tsabola. Conco anacenjeza makolo onse am'mudzimo kuti ana ao asapite kusewera ndi ana akumeneko, ndipo asalole alendo ocokera komweko kufika kuceza nawo. Amai anamveradi nasunga ana ao kumudzi, kwao koma mwana wina wamwamuna anazemba napita, kumudzi kuli nthendayo wosauza amace. Anadziwa kuti mace akanamletsa, ndipo anafuna kukatengako msenjere akauyesere mibvi ya kauta kace. Kumudziko anakomana nao anyamata anzace. Atasewera nao anabwerera kwao koma panjira anakomana ndi Bambo wace. Bamboyo poona msenjere anadziwiratu cire kumene mwanayo anapita nakwiya naye. Pofika kumudzi sanamulola kusewera ndi ana ena, koma anakhala payekha kunyumba milungu itatu kuona ngati nthenda ya tsabola iti imtulukire, koma anali ndi mwai, sinamutulukire ayi.

Patapita miyezi yina nthenda ya cikuku inafika ku mudzi winanso. Makolo anayesanso kuletsa ana ao kupitako, koma tsoka linagwera akulu ena, dzina lace Kampala. Iye analikusaka nyama ndipo pothamangira nyamayo, anapisa mwendo muuna nagwa nagulula kakolo. Mlongo wace anafika kucokera kuli nthenda kuja kuti asamale wobvulalayo. Anabwera ndi ana ace awiri ndipo anawo anayamba kudwala cikuku patapita masiku awiri. Pokhala kuti ana a Kampala analikugona nao m'cipinda cimodzi, Kampala anawaletsa ana ace onse kuti asacoke pakhomo pao kupita kumasewero ngakhale kusu-kulu. Ana a Kampala nawonso anadwala koma osati onse pamodzi ayi, koma wina atacira mnzace ndikudwala. Pokhala ana a Kampala anali anai nthendayo sinathe msanga ku banja lace.

Azimai amene analikuyang'anira ku bwala la ana, anakayika kwambiri kuopa kuti nthendayo ingaonekere mwa ana onse. Kusukulunso anawapenyetsetsa ana kuona ngati cikuku citi ciwaturukire koma ayi ndipo popita milungu yina nthenda inatha kumudziko. Dotolo atamva zimene anthu anacita ndi kuti analetsa kufala kwa nthenda ya cikuku anawatamanda nati:— "Mwapulumutsa ana anu ku nthenda yobvuta ndiponso pena ku imfa. Ku midzi yinayo komwe nthendayo inafala, ana ena anamwalira ndi cisoma cotsatira cikuku.

Indedi ndi kwabwino kupewa nthenda koposa ndi kuciritsa.

MUTU XI

ALENDO



Mateyu ndi Idesi anaona mtendere zaka zambiri nabala ana ena awiri. Woyamba uja Ndala tsopano anali wa zaka zisanu ndi zinai, Waciwiri mwamunanso dzina lace Misika wa zaka zisanu ndi ziwiri, womariza Linesi wamkazi wa zaka zisanu.

Ancembere anzace a Idesi akati, "Ha ! Koma muli ndi tsoka kuti mwana wanu wamkazi ndi wamng'ono. Akanayamba kubadwa iye bwenzi alikukusinjirani mphale ndi kulera ana anzace. Tsono atakwatiwa, mkamwini wanu akanathandiza kulima munda wanu." Idesi nayankha :— "Comweco ! koma pokhala pali bwalo la ana, amakasewerako ana ang'ono ndipo sindisauka nao. Ali ana omvera, a ulemu, namathangatana. Ngakhale mkuluyo akanakhala mkazi, sindikana-mulola kusinja akali wamng'ono pakuti kusinja ndi nchito yowawa yosayenera ana ang'ono." Koma akazi anzace anangoti, "Ndinu acumatu !

bwenzi Ndala alikuweta mbuzi.” Pamenepo Idesi anadziwa kuti amai ena amangoti ana ace aulesi, conco analongosola nchito zonse zimene ana ace amagwira kunyumba.

Anawo asamala zobvala zao ndi pogona pao ; athandiza kusesa masiku onse kunyumba ndi kubwalo ; apita ku sukulu masiku asanu pamlungu naphunzirako zambiri. Mwana atakula kuphunzira kumabvuta cifukwa akulu ali ndi nchito zina zambiri. Azimai anabvomera kuti ndi cocitsa manyazi, makolo akalephera kuwerenga, ana ao alikudziwa zonse.

Tsiku lina mkazi wa munthu wina, dzina lace Alifeyu, anadwala natengedwa kucipatala. Mateyu anafunsa Alifeyu kuti, “Bwanji nanga mudzakhale kunyumba kwathu ndi mwana wanunso kufikira mkazi aturuke kucipatala?” Alifeyu anabvomera nabwera ndi mwana wace wa zaka zitatu, dzina lace Manase, kudzakhala kwao kwa Mateyu. Idesi anasamala kabuthuko. Anakagoneka ku cipinda cija ca alendo. Nthawi yonse Alifeyu anakhala komweko, anaona ndi maso nchito zimene ana a Idesi anagwira.

Madzulo Misika anazungulira mabedi onse a m'nyumba natsitsa nsaru za udzudzu (mosquito-net), nazipenderera mozungulira mphasa zonse. Linesi anaseweretsa mwana wamlendo kufikira Idesi ataphika cakudya. Misika anatenga nsaru yoyera nayala patebulo, naikapo mbale ndi masupuni odyera cakudya ndi madzi akumwa. Pokhala Manase anali wamng'ono, Idesi anamudyetsa payekha, akulu ndi ana ena asanadye. Atadya anamusambitsa namugoneka kubedi. Ndipo pokhala kuti anali mlendo namalirira amai wace, Idesi anakhala naye pafupi mpaka atagona tulo timene.

Ndala akamthandiza Bambo wace kucotsa ndowe kukhola la mbuzi ndi kuyala maudzu ena. Ndowe anaika mu phompho nasanganiza ndi madzi kuti pakhale manyuwa (manure). Inde Ndala sanapite nazo mbuzi kubusa cifukwa Mateyu anaweta mbuzi zace motere. Anatenga cingwe cacitari nacimanga ku mwendo wa mbuzi namangirira ku mtengo umene anazika kumsipu kumene kunali mthunzi naikaponso madzi akumwa. M'mawa ndi madzulo anasintha malo a mtengowo kuti mbuzi zipeze msipu watsopano.

Alikusamala mbuzi Mateyu anapenya Alifeyu alikubwera kucipatala kumene anakaona mkazace. Alifeyu anati mkazace anali bwino pang'ono koma kuti anatonthola mtima podziwa kuti mwana wace ali ndi Idesi. Alikuceza Ndala anafika ndi mbuzi kuti azitsekere m'khola. Ana a mbuzi anatsekera paokha zazikazi nazitsekera pazokhanso kuti m'mawa adzazikama.

Amuna atatuwo atafika kunyumba Linesi anawacingamira nati:—"Ndakuikirani sopo ndi taulo kunyumba kosambira, ndi mai akuikirani madzi osambira."

Pamene analikusamba Mateyu anati:—"Musazizwe kuti mkazi wanga amadya nane limodzi patebulo, koma ndiwo mwambo wathu. Mkazi ndiye mnzanga ndi ana nawonso amadya nafe pamodzi pakuti adziwa ulemu wa pa caku-dya." Pakuyamba Alifeyu anacita manyazi paku-dya ndi mkazi cifukwa sanazolowera mwambo wotero koma posacedwa sanaganizapo kanthu.

Idesi anaphika nsima ndi ndiwo ziwiri. Ana-phika bowa wotendera ndi ntedza ndi anyezi. Anaphikanso nkuku pang'ono yotsalira kwa dzulo. Atadya ana anatenga madzi ndi taulo

kuti akulu asambe m'manja. Atatha anacotsa mbale nazitsuka nakaika mu kabadi. Alifeyu anadabwa kuti mwana wace Manase ali kuti, Kodi iye sadya? Idesi anamuuzza kuti Manase wadya kale phala la mkaka ndi papaya pang'ono. Anakhutadi cifukwa zina anasiya. Anati, Ana ang'ono ndimadyetsa paokha cifukwa sana-phunzire kudya ndi akulu, ndiponso amadya cakudya caocao cosiyana ndi ca akulu.

Alifeyu anapenya anyamata awiriwo alikupita kugona. Anabvula makabudula ndi malaya amene amabvala usana nabvala malaya amene amasungira kubvala usiku wokha. Zobvala zao za usana anapacika pa mauta, nakwecesa mano ndi kusamba nkhope ndi manja ndi mapazi. Asanagone anapemphera Mulungu kuthokoza zabwino zimene anazona pa usana, napemphera madalitso a Mulungu akhale pa onse am'nyumba. Ana ali m'tulo akulu anakhala pamodzi naceza za zonse zimene zinawagwera pofika nzeru zatso-panozi.

Alifeyu anakhala nawo mlungu wathunthu mpaka mkazace anabwera ku cipatala, ndipo anayamba kutsata citsanzo ca Mateyu, kuthandiza mkazace ndi kukweza banja lace.

Anakambira amuna anzace nchito za mitundu-mitundu zimene ana a Idesi anagwira kunyumba. ndipo anthu anakhulupirira. Inde citsanzo ndico ! Zam'kamwa zokha sizimveka.

MUTU XII

KUSOKA MALAYA



Anthu am'midzi analikudandaula cifukwa ca kuuma mtengo kwa nsaru ndi malaya m'masitoro. Nsaru zolimba zinauma mtengo kwa basi, ndipo posoketsa ku makina mtengo wace unapitirira kwenikweni. Idesi anakana kugula nsaru zosalimba ndipo analipira ndarama zambiri koma sanasoketsa ku sitoro, anasoka malaya kunyumba iye mwini. Zinthu zisanaume mtengo, Mateyu anamgulira makina yaceyace ndipo anasoka zobvala zonse zapabanja iye mwini m'malo mwa kutaya ndarama zambiri kwa Mwenye.

Azimai ena akati:—"Anzathu! muli ndi mwai. Taonani ife zimene tigula ku sitoro sizilimba komabe kuuma kwa basi!" Pamenepo Idesi anawauza kuti abwere ndi nsaru zao ndipo adzawafotokozera masokedwe ace. Tsiku lina akazi awiri anabwera ndi ana ao, wina mkazi, wina mwamuna, natenga nsaru zimene anagula kwa Amwenye. Idesi analinga misinkhu ya anawo,

nawathandiza kudula malaya ao. Anawasonyeza kuphatikiza kwace, azimai nasoka eni ace ndi manja ao. Mwina ndi mwina Idesi anawasokera pa makina yace koma maka anawalekerera kusoka okha, cifukwa anaphunzira kusoka ku sukulu ya akazi.

Nchito imeneyi inawakomera akazi ndipo pocuruka obwera ndi nsaru zao, Idesi anakopa mkazi wina wodziwa bwino luso losoka kuti awathangate. Pakuti azimai ena anatanganidwa ndi nchito zapabanja, amuna ao kulibe, anasowa nthawi yakusoka malaya athunthu ndi manja okha. Conco Idesi anati:— “Cabwino, mobvuta kusoka ndikusokerani pamakina koma mwina musoka nokha. Nditakusokerani mudzapereka kobiri limodzi caulere, kuika mu bokosi ili. Ndarama zace zikakwana, ndizitumiza kwa Bwana wa ku Boma, adzagwire nazo nchito zothandiza anthu amene anabvulala kunkhondo. Lero lomwe atsala anthu ambiri opunduka olira cithangato, ena opunduka maso, osaona, ena opunduka manja kapena miyendo, osatha kugwira nchito kapena kuyenda.

Bokosilo linalembedwa ndi mtanda wofira, ndico cizindikiro ca iwo othangata obvulala ndi odwala. Silinakhalire kudzala pakuti akazi anacuruka otsata cithandizo ca Idesi ndi makina yace. Citadzala analitumiza kwa Bwana wa ku Boma amene anawabwezera kalata yocokera akulu oyang'anira nchito ya Mtanda Wofira yakuti. “Talandira ndarama zanu. Zikomo kuti simunatiiwale.” Akazi ena amene amuna ao anapita kutari kunchito nawatumizira ndarama, anaziika ku Post Office Savings Bank kuti zisungidwe bwino kufikira zikakwanire kugula nazo makina yakusoka nawonso.

Eneresi, mkazi wa Alifeyu anafuna kusoka malaya a mwana wace. Kusitoro anaona nsaru yokongola yofiira yolembedwa timaanga toyera, koma mwini sitoro atamtsitsira nsaruyo kuti aipenye bwino, ha! inali yocepa m'bwambi, inakwana 27" basi. Anakumbukira mau a Idesi akuti, "Gulani nsaru yokula m'bwambi pakuti ndiyo yokwana bwino podula malaya." Apo Eneresi anasankha nsaru yobiriwira ngati masamba, ya maluwa oyerera. Nsaruyo inali yolimba ndi yaikulu m'bwambi mwace. Idesi anamuuzza kuti lupande limodzi kudza katheka ($1\frac{1}{4}$ yds.) lingakwanire malaya a mwana. Eneresi sanakhali kumariza kusoka malayawo, namubveka mwana wace. Mwanayo ananyada ndithu nakao-netsa kwa tate wace kuti, "Onani malaya andisokera mai wanga," Bamboyo natamanda mace kuti, Indedi mwaphunzira bwino."

Mkazi wina anacita mantha kusoka malaya iye mwini. Ati, "Ndikasoketsa kusitoro pakuti ndikayesa ndekha, ndigoononga nsaru." Popita kusitoro anati, "Ndifuna nsaru yokwana malaya a mwana wa msinkhu wa Manase." Mwini sitoro anati, "Cabwino, si iyi nsaru yabwino malupande awiri ndiponso mulipire makobiri ena osoketsa pamakina." Eneresi anafunsa Idesi kuti bwanji kusitoro amadya nsaru yambiri posoketsa. Onani ana a msinkhu umodzi koma wina amace anangu-lira lupande ndi katheka, wina anagula malupande awiri. Idesi anafotokoza kuti nsaru ikakhala yaing'ono, kufunika kusamala kudula kwace koma nsaru yaikulu angafulumire podula ndico cimene osoka kusitoro amacita osasamala zakuononga nsaru cabe. Ndiponso Mwenye akhumba malonda ambiri kuti phindu licuruke.

Tsiku lina Dotolo anabwera ndi malaya a

ana ena a cizungu kuti amai aone masokedwe ace. Panali tikabudula tokongola tosokedwa ndi kansaru kapamtima, ndi beresesi (braces) kumbuyo kuti mwana angabvale wopanda malaya, toyenera kubvala mwana wamkazi kapena wamwamuna. Nsaru yosokera tikabudula iti inali lupande limodzi lokha. Amai ena anakayika nati cobvala coterer mwana wamkazi sicingamuyenere koma Dotolo anambveka kabuthu kena ndipo onse anabvomera kuti cinamukhalira bwino ndithu. Akazi anakopedwa maka podziwa kuti nsaru inafunika lupande limodzi lokha.

Panalinso timalaya tobvala ana akhanda ndipo Dotolo anauza akazi kuti iwo amene anali ndi pathupi akanayamba cire kusokera malaya mwana watsopano. Ambiri anali ndi mantha nati, Kulaula kumeneko, koma Dotolo anati:— "Onani Idesi ana ace onse ali bwino ndipo iye anawasokera asanabadwe." Apo akazi anayamba kunong'onezana, wina nati kwa mnzace "Kasokenitu!" Pompo wina anaturutsa nsaru yoyera nati, Si iyi nsaru, ndidulireni malaya ndisoke. Akazi ena anzace nati, Ee! Ee! Ee! Koma Idesi anabvomera nati, Nzeru imeneyo! Onani ana anga. Anandiphunzitsa maleredwe ndi Dotolo omwewa. Mumvereni malangizo ao.

Conco anadula malayawo, mkazi nasoka bwino bwino napetera maluwa m'khosi ndi mumi-kono ndipo anali konzekere pobadwa mwana wace. Motere akazi anaphunzira kudzithandiza okha ndiponso kuthandizana wina ndi mnzace ndipo kumudziko kunali kumverana ndi kusan-galala.

MUTU XIII

KULEMBA MAKALATA



Mwana wa Anadimba anapita kugwira nchito ku Halale ndipo anada nkhawa kuti, “Kodi ndidzamuonanso mwana wanga Jameson? Suja anthu ena amapita maulendo otere osaonekanso?” Tsiku lina mtumiki wa mfumu anafika kunyumba kwao ndi kalata, “Landirani kalata amai. Khaya anakulemberani ndani?” Anadimba anali nje-njenje mantha nati, Conde, werengani. Ine ndakalamba, kuwerenga sindidziwa. Naye mtumikiyo sanadziwa kuwerenga bwino, anangodziwa pang’ono pokha. Koma kuti amaiwo angadzamuyese wosaphunzira, anati, Ah! ndatanganidwa nchito lero bwenzi ndakuwerengerani, koma kafunseni aphunzitsi.

Anadimba anapita nayo kalata kwa Mateyu ndipo iye anawerenga mau awa:—

Moni, Amai anga,

Ngati muli moyo, ndisekera kwambiri, Mulungu wandisunga bwino. Ine ndi anzanga

aja tafika bwino, ndipo tapeza nchito ndi Bwana wokoma mtima. Ndarama tirikulandira koma pokhala kuno zonse nzogula zokha, zirikupere-werabe.

Ndirikutumiza 10s. kuti mulipire munthu amange nyumba yanu. Mwezi wamawa ndiyembekeza zina, ndidzakutumizirani mugule bulanketi mudzifunda usiku. Nanga bwanji kodi munakolola zimanga kumunda kuja ndinalima mphanje? Nanga mlandu wa Afarisi ndi alamu ao unayenda bwanji? Funsani wina akulembere ni kalata, ndidziwe kuti mwalandira ndarama izi ndi kuti muli bwino.

Ndine Mwana wanu
Jameson Banda.

Anadimba anakondwera ndithu polandira kalata ndi kumva kuti mwana ali ndi moyo ndiponso polandira ndarama pakuti anada nkhwawa kuti, "Akandifolera nyumba ndani, ingadzandigwere ngati nyumba ya Anaphiri." Nyumba ya Anaphiri inagwa pokhala eni ace anasowa odzamu-folera. Inde Anadimba analikuumba mbiya napezako kakobiri kogula nako nsaru kamodzi-kamodzi koma zambiri zinamperewera. Mateyu anathandiza Anadimba namulembere kalata yopita kwa Jameson ku Halale. Anatenga pepala ndi inki ndi peni nalemba mau onenedwa ndi Anadimba kuti:—

Zikomo. Kalata ndi ndarama ndalandira bwino. Mlango wanu analikubvutika dzino koma anakamfunira mankhwala kuthengo ndipo lato-ntola. Mwana uja, mdzukulu wanga Jimu alikuleredwa mwacizungu koma ndakamfunira mphinjiri ya mphanvu kwa asing'anga ndipo mwanayo ali bwino ndi pano.

Anadimba anati, "Mulembenso anyani anandi-

thera cimanga kumunda kuja," koma Mateyu anatsutsa kuti, "Ndithu simunakolole kodi?", amai nabvomera kuti, "Ndakolola pang'ono," ndipo Mateyu analemba comweco. Analembanso, "Mlandu unamkanira Afarisi ndipo analipira £1 kwa alamu ace. Mundilemberenso msanga, ndidziwe kuti muli moyo. Onse kuno ati moni.

Ndine Amai anu
Anadimba.

Panali anthu ambiri osadziwa kulemba ndipo Mateyu ndi ana akulu a kusukulu anawalemba makalata ao. Akazi ena anasirira kulemba kuti akanalemba okha nkhani zakumtima zosafunika ena kudziwa. Conco Mateyu anayambitsa sukulu ya akulu madzulo. Ana akulu ndi ena odziwa kulemba ndi kuwerenga anali aphunzitsi. Mateyu anawakonzera maphunziro nawauza maphunzitsidwe ace.

Jine, mwana wa Anadimba anadzaphunzira ndipo tsiku lina anakondwera ndithu potumiza kwa Jameson kalata yolembedwa ndi dzanja lace. Analemba:—

Moni, alongo anga. Ndirikulemba
ndi dzanja langa.

Ndine mlongo wanu
Jine.

Pasanapite miyezi yambiri akazi enanso analikulemba okha makalata kwa amuna ao. Ngakhale ankhamba aja Anadimba anayesera kulemba dzina lace pa kalata yopita ku Halale. Koma anapukusa mutu nati, Ndakalamba ine, zandipitirira.

Mwezi ndi mwezi makalata anafika ocokera amuna amene anakagwira nchito ku maiko akutari. Mwambiri anaikamo ma postal order a ndarama. Koma cosangalatsa cacikuru cinali kuti anthu

akamva nkhani za abale ao m'malo mwa kungodandaula kuti khaya ali moyo?

Phindu lina la sukulu ya akulu pa madzulo linali kuti tsopano anaoneka mabukhu a malonda a mitundu-mitundu owerenga akulu. M'malo mwakuyesa kukumbukira nkhani zonse m'mutu ndi kumva zam'kamwa zokha, anatha kuwerenga zambiri zatsopano m'mabukhu. Kunali mabukhu okondweretsa kuwerenga, ena oseketsa, ena onena za miyambo ya anthu a m'maiko akutari, ena ofotokozero nzeru zina ndi zina zakale ndi zalero.

Inde kudziwa kuwerenga ndi kulemba kuthandiza koposa anthu onse, akulu ndi ang'ono, amuna ndi akazi.

MUTU XIV

MANKHWALA ONYENGA



Mkazi wina, dzina lace Aleya, anapita kuona mulongo wace amene anakwatira kumudzi kwina kutari. Ataceza kumeneko masiku oweregeka, a nabwera nso kwao koma anthu amene anamuona pofika anadabwa maonekedwe ace. Nkhope yace ndiyo ngati nkhope ya munthu wocita mantha. Anzace anamfunsu kuti, Kodi kuli bwino kumene mwacokera, iye nayankha, Indedi! Koma sanafuna kuceza ndi anzace.

Mwamuna wace nayenso anazizwa, pamene Aleya atapereka, cakudya, anati:— “Yambeni mwamwe mankhwala awa amunanga,” napereka cikho ca mankhwala. Mwamunayo, Kadete, anauka msanga nakwiya kwamбири, nati, “Kodi mkazi iwe umanyengana ndi wina kumene unapitako? Kapena uli kuti ndanyenga ndine? Nanga ukundimwetseranji mankhwala?” Aleya anakumata manja napempha

kuti, "Ndimvereni. Palibe amene wanyenga ayi. Ndithu mankhwala amenewa sali mankhwala amoto. Koma amene anandipatsa ati kuti aletsa mfiti kuti isatidye."

Kadete anapsya mtima kwabasi nakana kumva mau a mkazace naturuka m'nyumba nakagona kugowelo. Nkhani ya Kadete ndi mkazace inamveka m'mudzi monsemo, Idesi naye anamva nakaonana ndi Aleya kuti akamuthandize. Anapeza Aleya alikulira misozi nati, Mankhwawo ndagula kuti mfiti itisiye. Ndaononga ndarama khumi. Amene anandigulitsa anati amwe onse amubanja, pasakhale wina wosamwa cifukwa mfiti zidzalowa ujeju, koma amwe onse ndipo tsoka silidzagwera banja lanu. Ena ife tamwa koma amunanga okha ndiwo alikukana nandinamiza. Amene anandipatsa anati mankhwalawa ndi 'Nchape'.

Idesi anamfunsa, Kodi inu amai mukhulupira mau a mlendoyo kuti alikunena zoono? Anagokunyengani kuti akulandeni ndarama." Koma Aleya anaumirira nati, "Ayi ali munthu wodziwika. Onse akumudzi kumene ndacokako anagula mankhwalawa." Pakutero Idesi anapita kwao namuza Mateyu nati, Bwanji inu mupite mukaonane ndi Kadete? Mateyu anapita napeza Kadete alikudandaulira amuna anzace, iwo nanena, Zoono, zimenezi nzodabwitsa. Mwacita bwino kumusiya mkazi mpaka mlandu uturukire kubwalo. Koma Mateyu anatsutsapo nati, Aleya wangopusa, sananena bodza ngakhale kunyenga. Wabodza ndiye munthu amene anagulitsa mankhwalawo. Ndiye amene ali ndi mlandu wopita nawo kubwalo. Kadete sanafuna kubwera kwa mkazace nati poyamba apite kumudzi kumene anagula mankhwala, akamve zacitikako. Mateyu

pobwera kunyumba anati kwa mkazace, "Anthu awa angodzibvuta cabe ndi mantha a ufiti ndi zina zotere za mabodza." Idesi namukumbutsa kuti nawonso kale akanapasula banja lao cifukwa ca mabodza otero. Miyambo yakale siiwalika msa-nga. Yina yoipa inalikuletsa nchito yao yaku-phunzitsa anthu za moyo watsopano wa ukhonko.

Anthu ambiri akaperewera okha m'macididwe ao ndi m'makhalidwe ao salephera kucula wina kuti, "Uje ndiye wandicimwira kuti zoipazi zandionekera." M'malo mwa kulimbika okha ku nchito yokometsa moyo wao, angothamangira mankhwala onyenga. Mateyu ndi Idesi alikulingalira zotere, anamva Misika alikuitana, Amai! Amai! Pomfunsa kuti watani anati, Ndalota tulo ndipo ndacita mantha. Amace anampatsa madzi akumwa ndipo atamwa anati, "Gona, mwanawe, ulote zabwino." Posacedwa onse am'nyumbamo ndi am'mudzimo anali gone, osamva kanthu.

MUTU XV SING'ANGA



Akadete aja analawira mbandakuca ulendo wopita kumudzi kwa alamu ace. Pokhala kuti unali ulendo wa mabvuto sanatenga cakudya koma anakhulupira kugula mbatata kumsika popitirako. Anayendabe dzuwa lonse naturukira kumudzi, dzuwa litalowa.

Alamu ace anazizwa pomuona ndipo atalonerana anamfunsa kuti: “Kodi mbale wanga ali bwino?” Kadete nayankha, “Ndi zimene ndadzera ndikuuzeni. Zocita iwo cidzere kuno nzosadziwika.” Alamu aja, dzina lace Jere, anamuyang’anitsa Kadete komā poona kuti pali mlandu sanamuyankhe, ati ayambe amvetsetse. Jere anaitana mkazace kuti, “Afika alamu anga. Kufunika kuti ziri kumtima kwao zinededwe kwa akulu. Kandiiitanire akuluwo azimve angandinene kuti ndine ndatenga milandu kuno.”

Mkazi atapita Jere anaturutsa fodya wokoka nati, “Kokani, anzanga. Akazi atiphikira tsopano

lino. Masiku ano kwalusa kuno, mikango sico-kaku. Usiku walero mwana wa mfumu anadyedwa ndipo masana ano anaiona mikango kumadzi." Kadete anadzidzimuka ndi mantha nati, "Mwana wa mfumu wadyedwa kodi!" Jere anabvomera, "Indedi, nzacisoni. Anakaona mwana wodwala kumudzi kwina ndipo, pobwera kudambo kuja kwawirira ndinsenjere, mkango uli naye gwi! Ndiyo, 'Mayo! Mayo!' koma sanamulanditsa. M'mawa uno anapeza mutu wokha. Mlandu unenedwa mawa."

Pano Kadete anacita mantha naganiza mwa yekha kuti, "Ngati zaoneka zotere, ndalowa m'zoopsya, koma ndikati ndithawe tsopano angandiyese ine mfiti kwa eni ace kuno." Ali kulingalira izi, Atate a Jere anaturukira nakhala pansu. Jere anayamba nkhani yace nati, "Alamu anga ali kubvutika mtima ndipo pokhala izi nzosanena ana ndati koma akulu azimve atiweruze." Akulu nati, Nenani. Conco Kadete analongosola nati, "Mwezi wathawu mkazi wanga, mwana wanu anabwera kwa ine nati ndimulole akaonane ndi akwao ndipo ndinabvomera. Milungu inai iyo ndinali ngati wamasiye kumaphika ndekha ndi kugona pa ndekha. Mwana wanu anabwera dzulo nati, Imwani mankhwala angawa, mudyeye cakudya canga. Koma munthu sangamwe mankhwala popanda cifukwa, ndipo ndabwera kukufunsani pamenepo."

Atanena panali cete! Aphongozi anatambalitsa dzanja nalandira fodya wa Kadete nakoka. Popita kanthawi anati, "Mwana wa Yobe anapita ku Halale nabwerako mwezi wathawu. Anabwe ra kubwalo nauza anthu kuti, "Inu mutayiranjini ndarama zanu kugula mankhwala ndi mipinjiri yopanda pace? Ine ndiri nawo mankhwala a


mphamvu kwa basi, oposa mankhwala ena ali onse. Tayani mipinjiri yanu, mugule mankhwala awa. Mfiti zikuopani, zikulekani. Gulani 5s. ali yense nimupulumuke zowawa."

Ife tinaona kunenepa kwace ndi cuma cace ndipo tinamukhulupira. Ambiri anagula mankhwala ace ndipo mkazi wanu anagula nayenso, ena nati atenge kwa inu" Kadete anati, "Ndamvano, ndizo zimene anandiuza ine koma ndinati angonama. Nanga munthu nkukhulupirira nkhani yotere popanda umboni? Kani mwana wa mfumu sanamwe mankhwalawo apo wadyedwa ndi mkango?" Koma akulu anati, "Palibe munthu m'mudzi muno sanamwe mankhwalawa, koma mkazace wa Yobe anadwala cibayo, nyani zinatha cimanga m'minda ndipo tsono mwana wa mfumu anadyedwa ndi mkango. Ndiyono tazindikira kuti watinyengadi. Wonyengayo wathawa koma apolisi alikumufuna m'midzimo kuti amuweruze mlandu wakulanda ndarama monyenga."

Kadete anapepeza kuti, "Zikomo, ndamva. Ndiribe mau ena." Koma kumtima anati akamseke mkazace kuti nzeru zanzi zotaya ndarama pa mankhwala acabe. Pamenepo akazi anafika ndi cakudya ndipo ali pa cakudya anamva mkango ulikulira pafupi. Mwamsanga anamariza cakudya nalowa m'nyumba nadzitsekereza molimba. M'mawa mwace anamva kuti mafupa a munthu anapezedwa m'thengo kufupi ndi mudzi. Cisoni pokaona anapeza malaya a mwana wa Yobe ali ng'ambi-ng'ambi, miyazi pyu! Uja amati athawe anagwidwa ndi mkango.

Kadete anapita kwao nafikira ku nyumba ya Mateyu nati, "Zikomo mwanena zoona, bwerani mudzandipepezere mkazi wanga." Aleya ana-

kondwera kwambiri kuonanso mwamuna wace
 ndi kudziwa kuti anamkhulukira kupusa kwace.
 Koma anacita manyazi pakumva kuti ananyenge-
 dwa nataya 10s. cabe. Mwamuna na ngoti, "Izotu !
 ulekeranji kumvera ndi kutsata maphunziro akusu-
 kulu ndi ku misonkhano ya akazi?"



MUTU XVI ACEZA KWAO



Tsiku lina Idesi anati kwa Mateyu, “Koma ndiyenera ine kupita kwa amai ndikawaone. Tsopano akalamba. Nkhani ija yakale ya ana sangaiturutsenso cifukwa ana tiri nawo. Conco atatseka sukulu anakonza ulendo wopita kwao. Katundu atalongozalongeza, Mateyu ndi Idesi ndi ana ao atatu ananyamuka kukacingamira baasi (bus) kumseu. Idesi anati “Isadzati galimoto yadzala anthu, poti ndi dzuwa ndi pfumbi tikati tipsinjanenso tibvutikadi.”

Galimoto inacedwa kufika ndipo anadikira kumthunzi. Linesi anayamba kudandaula ndipo Idesi anapatsa mwana aliyense nthoci adye. Alikudya Ndala anati, “Onani kapusiko m’wambamo.” Kapusi kamasendera kuti pena kangatole nthoci koma nthawi yomweyo galimoto inamveka ikubwera dididi kumseu ndi kapusiko kanathawa. Poima galimoto munatsikamo mwa-

muna ndi mkazi alikukwekwereza cimtanga comangiridwa nsaru pamodzinsu ndi cikhwere ca nkhuku.

Mateyu anakapangana ndi eni galimoto za mtengo wolipira ana, koma zonse zinakonzeka bwino ndipo onse anapeza malo okhala ndi malo oika akatundu. Ana anakondwera kwa basi pokwera mugalimoto. Linesi yekha ndiye anacita mantha nakhala pa maondo a mai wace. Atayenda cinthawi anaimitsa galimoto kuti anthu aongole miyendo ndi kudya cakudya cao. Mateyu anaturutsa botolo la madzi a mandimwe kudzanso mbatata zooca pamoto ndi nthoci ndipo onse anadya namwa nakhuta. Atayendanso maora ena atatu anaona nyanja iri nyezi-nyezi, woyendetsa galimoto naliza lipenga kuti anthu a kumeneko adziwe kuti afika. Onse anaturuka aone afika ndani m'galimoto ndi kuti athangate alendo kunyamula akatundu ao.

Idesi anaona amace ndipo anathamangirana, misozi m'maso cifukwa ca kukondwa. Ambuyace anamlandira Linesi mosangalala ndipo anthu ambiri ena anadzalonjera Mateyu ndi Idesi nathangata kusenya akatundu. Panali cipokoso ceniceni, "Moni! Moni!" onse kunena pamodzi. Bambo wace wa Idesi sanaturuke kumseu cifukwa ca kubvutika poyenda pakuti anakalambadi, koma anali pakhonde panyumba kuwadikira.

Anapeza madzi okonzekera kale kuti asulukute pfumbi akadye bwino. Ambuye a ana akangowanyamula ana nati, "Ana anga, ana anga!" ndi kuti "Ee, idyani, idyani," ana atakhuta kale. Ananyadira adzukulu ao kwambiri kuti inde ngamphamvu ngakhale aleredwa mwambo wacilendo. Mateyu anaturutsa mphatso zace zimene anawatengera akuluwo, ndipo pamudziponse panali cisangalalo ceniceni.

MUTU XVII

ZAKALE NDI ZATSOPANO



Akulu alikuyang'ana mphatso zao Linesi ananong'oneza Mbuyace kuti afuna kucimbudzi. Ambuye anazizwa nati, "Nciani? Ha! ufuna kupambuka. Pita uko kutseri kwa khola la mbuzi." Linesi anapitako koma wosaona cimbudzi, anangopeza malo oipa, onunkha. Conco anabwera nati. "Sindinaone cimbudzi." Banja lonse linati cete, manyazi, koma Idesi anapita naye mwanayo nanyamula khasu nati, "Ambuyako akalamba ndipo sanakumba cimbudzi koma iwe uzitere. Tenga khasu, ukumbe kadzenje ndipo ponyamuka ukwirirepo ndi khasu.

Idesi anathandiza amace kufotokoza malo ao ogona. Pokhala kuti anadziwa kuti amace analibe nsaru za udzudzu, anatenga zao zakwao pamodzinsu ndi zina zatsopano zopatsa makolo. Panalibe windo m'nyumba monsemo ndipo ana analephera kugona tulo cifukwa anazolowera malo a mphapo yabwino. M'nyumba munatentha

udyo conco Mateyu anatenga cikha ca nkuku nang'amba naifutukula napacika pakhomo namangirira usiku kuti musapite fisi kapena nyalugwe. Cikha cimodzi sicinakwane koma anatenga ziwiri nakomaniza. Tsono banja lonse linapeza tulo cifukwa anatopa ndithu.

M'mawa mwace apongozi a Mateyu anamuthokoza nsaru za udzudzu zija, nati:—"Nzabwino zimenezi. Usiku tinafundula bulanketi kumutu koma osalumidwa udzudzu. Pokhala kunatentha kwambiri tinagona bulanketi mucuuno mokha koma osalumidwa. Nzothandiza ndithu nsaru zimenezi." Mateyu anabvomera nati kunyanja kutenthadi. "Bwanji ndikuikireni mawindo m'nyumba yanu, uku awiri, kwinko awiri?" Bambo sanafuna mawindo, koma amace a Idesi anamupempha alole Mateyu aike mawindo cifukwa ana anazolowera kugona m'nyumba yotero ndipo mfiti sizilowamo kuwaphweteka ndipo Bamboyo anabvomera.

Mateyu analemba wanchito wakumuthandiza, ndipo Ndala ananyamula mcenga wakukonza makoma atagumula poika mawindo. Feremu (frame) zace zinali mitengo yosasema ndipo anakhomapo nsungwi kuti zirombo zisalowe. Anadula mphasa zokwana kuphimbapo madzulo koma masana anakulungira m'mwamba kuti mulowe kuunika. Anamariza zonse kusanade. Bambo anabvomera kuti "Inde ndiponi nyumba yasiyana kutentha yosanga kale, koma udzudzu udzalowa wambiri pobookapo. Anthu kuno akati agone amayamba kufukiriza utsi m'nyumba monse, natsekaponse pamene udzudzu ungalowe." Mateyu anati nzoona. Koma kuti kunali nzeru zina zimene angacite kuononga udzudzu, akalambula maudzu m'mudzi ndi kuleka kubzala zinthu

zowirira pafupi panyumba ndi kutaya kapena kuyendetsa madzi onse ogona pafupi pamudzi, adzaononga udzudzu wambiri. Abambo a Idesi analikumva msana, anali cigonere mlungu wa thunthu ndipo mkazace anamtumikira. Atakhala bwino pang'ono, poturuka panja anaona Idesi alikuzira cimbudzi catsopano cimene Mateyu anamanga.

Akulu ena anaseka nati:—"Kodi muti mphunzitse mkalamba gule latsopano, maondo atauma kale?" Komabe anazolowera cimbudzico ndipo masiku onse Idesi anacisamala kuti musanunkhemo ndipo munalibe ncence monga kale. Asanacoke mphwace adaphunzira masamalidwe ace. Mlongo wace ataona zatsopanozo, zinamkomera ndipo anayamba zomwezo kunyumba kwace. Comweco pang'ono-pang'ono citsanzo cimodzi cabwino cinaphindula mphatso zabwino m'nyumba za anthu ena.

MUTU XVIII

KUNYANJA



Masiku onse ana anauka m'mamawa napita kusewera kunyanja pamodzi ndi ana anzao. Makolo anawauza kuti asapite okha kufupi ndi nyanja, angagwidwe ng'ona. Posewerana anayimba nyimbo napokosera napirikitsana.

Ndala ndi Misika sanadziwa kusambira m'madzi koma anzao anawaphunzitsa. Mwina anzao akawaseka kuyesa kwao kusambira nati sadziwa zonse ngakhale anapita kusukulu masiku onse. Makamaka Misika anakondwa ndithu, ataphunzira namaitana

ana ena kuti, "Mundione, ndacokera uko kutari m'madzi mokha."

Masewera ena amasewera kumadzi ndi
awa:—

Panali magulu awiri a ana. Gulu lina liyimbira linzace kuti, "Mcere". Iwo nabvomera kuti, "Woyenga." Oyambawo nayimba,

“Wapsya”, anza nati, “Ukalipo”. Atayimba kawiri nyimboyo anapirikitsana m’madzi mokha. Amene anathawira kuntunda ndiwo ogoma.

Masewera ena ndiwo oona ndani ati amire m’madzi nthawi yaitari kuposa anza. Ana oyang’anira anaomba manja nayimba nyimbo, wina alikuwerengera ciwerengo cace. Mmodzi wa asiwani a Ndala anapambana namira mpaka anzace anafikira ciwerengero ca makumi-khumi, koma ena anangofikira makumi asanu okha.

Alikusewera conco, anamva Linesi alikulira, “Mayo ine” ! alikupuluputa m’madzi. Ndala anamuthamangira namturutsa. Mwanayo anati atsanze anzace namiza mutu wace nazondokera mommo nacita mantha.

Akulu ena analola Ndala apite nawo nthawi zina mubwato, ndi kuyesa kupalasa. Paciyambi anaona kubvuta ndi pang’ono pomwe akanataya copalasila cace. Tsiku lina anapenya ng’ona iri pamcenga m’mbali mwa mabango koma itamva bwato lirikuyandikira, inathawira m’madzi. Kuyanyako kunali mbalame zambiri ndipo tsiku lina Mateyu anawaphera mabakha a m’madzi akadyere nsima.

Usiku womwewo, pa nthawi yakugona panali cipokoso cacikulu kugombe kunyanja. Ana anati : “Nciani cimeneco”? Ambuyao naseka nati “Mvu imeneyo. Iribe kanthu, sitiiopa, koma ikabwera m’munda, imaononga mbeu.” Atakhalako milungu iwiri, Mateyu anauza Ndala kuti angatsagane naye usiku kukagwira nsomba kunyanja. Tsiku lonselo Ndala anapenya asodzi alikukonza ukonde wao ndi mabwato ao ndi kupanga miyuni ya maudzu ndi mabango, cifukwa anati asodze usiku ndi miyuni. Madzulo anthu ambiri anabwera kuona mabwato alikunyamaka. Mateyu

analowa m'bwato lina nakhazika Ndala pafupi naye namucenjeza kuti asabvutitse asodzi. Anapalasa m'mbali mwa nyanja m'mene anadziwa kale kuti munali nsomba. Atafikako anaturutsa ukonde wao coteru kuti ukonde unatandala kucokera bwato limodzi mpaka ku bwato laciwiri. Atacera ukonde anayatsa miyuni ndipo nsomba zinafika zambiri kutsatira kuunika kwa miyuni. Ndala anazona ziri nyezi-nyezi m'madzi, zinali zokongoladi. Usikuwo anagwira nsomba zambiri nabwera nazo kumudzi.

M'mawa mwace kunali cinchito kugombe kunyanja, malonda a nsomba. Nsomba zina anazigulitsa zaziwisi koma zina anawamba. Ena ogula anaika nsomba zao m'madengu akulu namangirira pa njinga kuti akagulitse kutari. Mateyu anamuza Ndala kuti kuli njira zina ndi zina zakupha nsomba. Anati kuti posodza ndi miyuni amagwira nsomba zambiri zazing'ono zosayenera kugwira ndi kudya. Akati asodze coteru kawiri-kawiri makamaka pamene nsomba zisanakule, bwenzi anthu adzasauka njala ya nsomba.

MUTU XIX

ABWERANSO KWAO



Pakuti nthawi yobweranso kwao inali pafupi, Idesi anati aonane ndi aphunzitsi ace akale amene anamulozera njira yatsopanoyi, ndipo anapita onse ku Mission. Kumeneko akucipatala anatamanda Idesi maonekedwe a thanzi a ana ace nati aleredwa bwino ndithu. Idesi anati kuti kunali bwino kuti anacoka kale pamene ana oyamba kubadwa aja anamwalira cifukwa ku mudzi watsopanowo anapeza mtendere ndipo amai ace aona adzukululu ace.

Aphunzitsi anamfunsa kuti ana ace adzacita ciani atakula. Idesi anayankha kuti afuna iwo abwere ku Mission, apitirire maphunziro ao monga iye ndi Bambo wao anacita. Koma za nchito imene ati agwire, akakula anati, "Sindi-dziwa, pena kuphunzitsa, pena ku nchito ya cipatala, pena umisiri wa mtundu uli wonse. Adzasankha okha akakula nchito imene iwa-konda." Mphunzitsi wakale wa Idesi anati,

“Nzoona, cifukwa mukati mukakamize ali yense ku nchito yosaifuna mwini, nchitoyo sigwirika bwino.”

Idesi anapeza anamwali ambiri alikuphunzira ku sukulu yace yakale. Ena a iwo anali ana ang'ono pamene Idesi anacokako. Mphunzitsi anati auze ana a sukulu za nchito imene analikugwira ku sukulu yace kutariko. Anawauza za miso-nkhano ya akazi, ndi za bwalo la ana ndi kuti tsopano akazi ena analikugwira nchito zaozo paokha, osangoyembekeza Azungu awacitire. Anati: “Nchitoyi iri yobvuta koma ine ndiri ndi mwai, ndiri ndi mwamuna wabwino amene andithangata. Popanda iye pena ndikanalephera. Ndiyembekeza kuti nanunso mudzapeze amuna amene adzakuthangatani ndi kuti mudzagwire nchito yanu pamodzi. Dziko lathu lidikira akazi ophunzira onga inu. Maka lisowa mabanja enieni a Cikristu kuti ana nawonso akulire ndi miyambo ndi makhalidwe abwino.

Posankha mwamuna kumbukirani kuti mnyamata wozemba sukulu, wocita ulesi pa nchito, wopanda ulemu kwa makolo ndi kwa akulu, ameneyo ndi mwamuna wosayenera konse.”

Atanena mau awa Idesi anatsazikana nawo onse a ku Mission nabwerera kwao. Bwino lace anayamba kukonzera za ulendo wopitanso kwao kuti ayambenso nchito ya sukulu. Ana sanafuna kupita cifukwa kunyanjako kunawakonda komabe analikuyembekeza kukaona ana anza akusukulu, awafotokozere zonse zimene anacita kunyanja. Idesi anatsazika makolo ace nati:— “Mubwere tsiku lina mudzaone kwathu.”

Abwenzi ao ambiri anapita kumseu kucingamira galimoto, anatenga nkhu, nsomba, maungu, mafuta a ntedza ndi zakudya zina coteru kuti

mwini galimoto anati :— “Kodi mukuti inu nokha mukwera pa galimoto.” Koma malo anapezeka a onse. Ananyamuka ulendo nafika kwao madzulo. atatopa ndithu. Idesi ndi ana ananyamula katundu wina ndipo Mateyu anasenza zonse zina zotsala.

Anakondwera pofika kunyumba ndipo anadya cakudya cophika anza akumudzi amene anathokoza kuwaonanso ali ndi moyo wabwino.

MUTU XX

KUMANGA NYUMBA



Mmodzi wa abwenzi a Idesi anali ndi mwana wamkazi, namwali wotomera kwa mwamuna wogwira nchito ku cipatala ca ku Mission. Anati ukwati ukhale ku chalici pokhala onse awiri anali Akristu.

Namwaliyo, dzina lace Alesi, anaphunzira kusukulu ya Mateyu. Atamariza sukulu anathandiza amace kumunda ndi m'nyumba ndipo bwino lace analowa nchito yolera ana a Azungu ku Mission. Pamene ana a Azungu anapita ku sukulu ku England Alesi anaganiza za ukwati kuti akhale ndi banja lace.

Mwamunayo anapatsidwa malo omangapo nyumba ndi munda koma caka coyamba anathandiza kulima munda wa apongozi ace. Pakuti kwina anali kunchito ya cipatala, kwina kumanga nyumba, kwina kulima, mwamunayo anatangani-dwa nchito. Anagula zitseko ndi mawindo kwa mmisiri wina wakumudzi. Namwali anathangata

kutenga maudzu. Mitengo ndi nsungwi anadula naika pamalo pamene ati amangepo koma analamba mmisiri wina wakuumba njerwa. Njerwa zinali zosaoca pakuti nkhuu zinasowa.

Cinamukayikitsa ndico kukula kwa nyumba ndipo anapita kwa Mateyu kufunsapo cifukwa onse anadziwa kuti nyumba yace inamangidwa bwino. Mateyu anati, "Nyumba yangayi ndinamanga malinga ndi cifuniro ca mkazanga. Pakuti mkazi ndiye asamala zonse zakunyumba, ayenera kucula umo aifuna nyumbayo." Koma mwamunayo anakayika nati, "Ndingamfunse bwanji mkaziyo? Akati afuna cinyumba cacikulu, ine ndarama zace ndikaona kuti? Ndidzangocita manyazi." Alikunena conco, Idesi analowa m'cipinda momwe amuna analikucezamo ndipo Mateyu anamfunsa za nkhanio nati:—"Nanga inu amai, muti bwanji?"

Idesi anabvomera mau a mwamuna wace kuti Alesi akanafunsidwapo ndikuti onse awiri adzambvane za mamangidwe anyumba ndi za ndarama zofunikapo. James, pofuna kusacita manyazi, akamanga nyumba yaikulu ndi kutherapo ndarama zace, Alesi anganene kuti: "Mwamuna wanga ngwa cuma" nadzazizwa m'tsogolo James akamuza kuti, "Sindingakugulire cakuti ayi: ndarama zogula ndiwo mwezi uno nzakuti basi." Iye adzati, wakwatira womana, wosamukonda. Komanso James akamanga kanyumba kakang'ono, kapena kuikamo zitseko ndi zipangizo zacabe, adzangotaya ndarama zace nadzacurukitsa nchito ya Alesi. Pomwepo anapangana kuti onse awiri abwere ku nyumba ya Idesi akayese kumvanapo bwino.


Pamene anakomana onse pamodzi m'mawa mwace anapangana zonse za kukula kwa nyumba

ndi za ndarama zimene angaononge pakumanga ndi pakugula zipangizo ndi ziwiya za m'nyumba. Ananenanso zakumanga kitchini ndi cimbudzi ndi za kucuruka kwa zipinda, ndi zitseko ndi mawindo. Mateyu ndi James anawerengera kucuruka kwa njerwa ndi mtengo wao, ndaramanso zogula zitseko ndi mawindo ndi zolipira anchito othandiza kumanga nyumba. Anapeza kuti ndaramazo zinacurukadi ndipo ponenanso ndi akazi, Alesi anati, "Cabwino, tiyeni tisiye kumanga cipinda cija cakukhonde. Tikaona ndarama zina m'tsogolo, sikubvuta kumanga cipinda capakhonde. Tisangoononga ndarama zonse tsopano." James anakondwa kumva mau awa nati m'mtima mwace, "Komatu ndapeza mkazi wanzeru."

Mateyu anathandiza James kulemba nyumba, kuti ayambe cire kukumba poika maziko ace a miyala. Popita milungu yowerengeka makoma anamangidwa ciriri ndi maferemu a zitseko ndi mawindo anaikidwa. Amuna anzace anathandiza kumanga denga ndi kufolera nyumba, akazi nathandiza Alesi kupoma ndi kuzira.

Alesi analikusoka nsaru za ukwati, zina zobvala iye mwini, zina za patebulo ndi zapabedi ndi zina zoika pamawindo. Idesi anathandiza kusoka malaya ace oyera a ukwati kudzanso nsaru yobvala pamutu. Dona dotolo anati wophika wace aphika keki ya ukwati yoyera. Comweco zonse zinakonzekera ukwati.

MUTU XXI UKWATI



Pofika tsiku la ukwati anthu onse am'mudzimo anasiya zinchito zao nasonkhana kuti asangalale pa ukwati.

Alesi anakongola kwa basi ndi deresi (dress) yace ndi capamutu cace coyera. M'manja munali maluwa a ku munda wa Idesi. Anamwali anzace omuimirira pa ukwati anabvala malaya a silika (silk) a maluwa nawonso anali ndi maluwa m'manja. Akazi anzace anamperekeza kucokera kunyumba kufikira ku chalici, James ndi amuna anzace atafika kale ku chalici. Alesi anali dwi!

malinga ndi mwambo wa anthu kuti asamasekerera pa ukwati, koma m'mtima mwace munali cimwe-mwe cokha.

Atakwatitsidwa anaturuka, Alesi alikugwira mkono wa mwamuna wace malinga mwambo wacizungu. Abwenzi ao anawanyamulira simbulela (umbrella) kwaphimba dzuwa. Iwo awiri

anayenda nkhope dwi ! koma anza onse analiza mapenga, naluluta, nayimba nyimbo, ena nabvina panjira kusonyeza kusangalala kwao. Mkalamba wina anali ndi mfuti, naiomba.

Kunyumba kwa Alesi anayala phwando lalikuru. Anabwerekka matebulo ndi mipando ku nyumba za anansi onse kudzano kusukulu. Pa matebulo onse panali maluwa, mbale ndi makapu ndipo pa tebulo la mkwatibwi panali cikeke cacikuru conyezimira suga. Kunali cinchito kugawira anthu onse tii, buledi (bread) ndi makeki, kudzanso mpunga ndi nyama. Alendo osaitanidwa ku ukwati, anakhala pansu pa mitengo nalandiranso mpunga ndi nyama.


A banja la Alesi ndiwo analipira phwandoli, ndipo onse anabvomera kuti ukwati wotere sanauone ndi kale lonse kumudziko.

Alikudya mpingo wa anyamata ndi anamwali anayimba nyimbo zokondweretsa, zotamanda mwamuna ndi mkazi okwatitsidwawo. Pambuyo pace anabvina ndipo pomva ludzu anamwa madzi a mandimwe ndi tii. Madzulo James ndi Alesi anaperekezedwa kunyumba kwao ndi nkhoswe zao ndi akulu ao. Akuluwo anawalangiza za makhalidwe ndi mayendedwe oyenera mwamuna ndi mkazi pabanja pao.

Akucikazi anatamanda namwali wao kunena za kukoma mtima kwace, kumvera kwace, ndi nchito zace. Akucimuna nawo anatamanda mwana wao namunenera zabwinonso. Yense atamariza kulankhula anaika ndarama mumbale patebulo, zikhale mphatso kwa okwatiwawo. Atawasiya, anthu ena onse anakondwera pamodzi kubwalo nati:— "Koma ukwati umenewu ndi wokondweretsadi."

MUTU XXII

NGOZI



Tsiku lina Ndala anapita ndi anyamata ena kuthengo kukadya nku-ndi. Mitengo ya mikundi njaitari, nthambi zosakhalira kuduka akati azikwerere. Zipatso zace kunja kuli kwakudera koma m'kati muli mofiira ndi nthanga zazikuru. Ana maka akonda kudya nkundi ndipo mano ao ndi malaya omwe afiira nazo.

Ndala ndi anzace anakwera mitengo kuti acere nkhundi ndipo Ndala atapita pa kanthambi kocepa pamene anaona zina zazikulu zakupsya, tsoka lina-mgwera. Nthambiyo inatyokat yotyoty, mwanayo phofo ! pansidi ! anzace, Mayo ! Mayo ! koma Ndala yekha, cete ! wakomoka. Tsinde la nsungwi linamulowa mwendo ndipo mwazi unali pyu-pyu ! Mnyamata mnzace anamkweza mutu namutsamila pa malaya ace, wina natenga luzi namumanga mwendo kutseka mwazi, ena nathamanga kumudzi

akamuuze Bambo wace. Atawapeza anati, "Thamangani, Ndala wagwa m'mwamba, wako-moka."

Mateyu anathamanga kuti amunyamule mwana, Idesi nafulumira kutereka madzi amoto nafunira nsaru zomanga bala ndi mankhwala omwe anaphunzira kucipatala. Zonsezi anaika patebulo pamodzi ndi beseni ndi taulo, pafupi pa bedi la Ndala. M'bedi anaikamo mafuwa otentha atakulunga masanza kuti pabedi pafunde bwino mwana wokomokayo angazidwe.

Amuna ena anamthangata Mateyu kunyamula mwana, akazi ena nathangata Idesi kukonza zonsezo. Pamene anafika naye Ndala kunyumba, Misika ndi Linesi analira kwabasi kuopa maonekedwe ace. Mkazi wina anapita nawo kunyumba kwace nawatonthoza kuti asabvutitse makolowo. Wina anatsira madzi amoto m'beseni, Idesi alikumgoneka mwana pabedi. Anacotsapo nsamilo namugoneka cagada koma mutu anapendeka kumbali kuti malobvu ndi makhololo aturuke m'kamwa angatsamwe nawo.

Anamuyang'ana thupi lonse kupenya mabala ace namufunditsa mabulanketi. Anatsupuka nkhope, manja ndi maondo. Bala lapamwendo linaleka kukha mwazi cifukwa ca kumangira luzi lija.

Makolo anati apite naye msanga kucipatala nakonza ulendowo, amuna nalinganiza macila, Idesi alikutsuka mabala. Luzi lija anamasula pang'ono nalola mwazi kuyenda pang'ono namanganso kuopa kuti mwendo wonse ungaume cifukwa ca kuthina. Anatsuka balalo ndi madzi otentha ndi mcere ndi nsaru yoyera namanganso zolimba ndi nsaru ndi thonje. Anatumula mwendo pa nsamilo yolimba kuti mwazi ubwerere ku mtima, wosapitira ku balalo.

Ngakhale Ndala anali wokomokabe koma mtima wace unalikugunda mwamphamvu. Atatha kutsuka bwino ponse potsupukapo, macila aja anakonzeka opangidwa ndi cikhwere cacikulu ca nkhuku, ca mabango ndi nsungwi. Zonse zamangidwa zolimba kuti mwana agonemo tambalale. Anapindira mabulanketi pamacilapo, namugonekamo, mwendo uli pansamilo namufunditsa mabulanketi ena. Asananyamuke, Idesi anamasulanso luzi lija pang'ono nalimanganso. Panjirapo anateronso kawiri kuopa kuti mwendo ungaume, asanafike kwa dotolo. Lifeyu uja ndi mkazi wace anati adzayang'anira kunyumba ndi kudyetsa ana pamene ali kucipatala. Anati: "Suja inu munaticitira cifundo kale muja tinali m'mabvuto. Lero tikuthandizani inu."

Amuna anathandiza kuzenza macila ndipo anayenda msanga. Panjira Ndala anagwedeza mutu kamodzi koma sananena mau. Atafika kucipatala dotolo anabwera nayang'ana mamangidwe a mabala ace. Anatamanda Idesi nati, "Mwacita mwanzeru ndithu, mwana wanu adzacira bwino koma mumusiye agone kuno kucipatala. Musade nkhawa, timusamala bwino. Mukapumule tsopano ndimubwere titamumanga bala."

M'mawa mwace Ndala analikupenya ndi kulankhula bwino koma pamutu ndi pabala panalikumpweteka. Mateyu anabwera kumudzi, ku nchito yace ya sukulu koma amai ace anatsala namudikirira kufikira mwanayo anatha kukhala tsonga pabedi ndipo nayenso anapita kwao. Anapeza ana ena aja alikukondwa kunyumba kwa Lifeyu.

Idesi anawathokoza abwenzi ace Eneresi ndi Lifeyu nati:—"Zikomo cithangato canu. Mwandikhazitsa mtima ndithu. Mwandizimira ndebvu."

MUTU XXIII KUCIPATALA



Makolo a Ndala anagona kwao kumudzi koma anamuyendera kucipatala tsiku ndi tsiku. Patapita mlungu umodzi kunafika munthu kukhomo kwa Mateyu kunena kuti kumseuko kwafika ankhamba otsikira pa galimoto aliku-funsa kuti:— “Kodi kunyumba kwa Mateyu nkuti?”

Idesi anathamangirako napeza kuti ndi amai ndi atate ace abwera kudzaceza. Kwao anamva mbiri kuti Ndala analikudwala nati, Tipiteko, tikamuone mwanayo. Anati kuti kunyanja anacoka cetecete osauza anthu ena angawaletse kuti, mwakalamba mungapwetekedwe mugalimoto. Kuyenda anayenda bwino cifukwa oyenda mugalimoto sanacuruka. Idesi anakondwa ndithu kuwaona koma anafunsa:— “Kodi abale athu akumudzi sadziwa kuti mwanyamuka?” Makolo anati, “Pano adziwa cifukwa galimoto litayamba kuyenda tinaitanira ena akwathu opita mumseu

kuti anene kumudzi kuti tapita.” Idesi anati adzatumiza lamy kuwadziwitsa kuti mwafika bwino, angade nkhawa.

Alikupita kunyumba anafunsa za Ndala namva kuti alikukhala bwino koma kuti alikugonabe kucipatala. Akuluwo anazizwa kumva kuti anamusiya mwanayo yekha. Idesi anati kuti kucipatala kuli malo abwino a antha odwala, cakudya cabwino ndi anthu okoma mtima omuyang'anira, ndipo kuti iye mwini kapena Bambo wace amamuyendera masiku onse.

Posacedwa anamva galimoto liri di-di-di kubwera. Ayang'ana aona kuti dotolo wafika ku msonkhano wa akazi. Makolo anafunsa kuti ndani alikusamala Ndala popeza dotolo wamusiya nati, Kodi siizi timanena kuti alendo sangasamale? Dotolo anaseka nati, Mawa ndibwera ndikutenge ni kucipatala mugalimoto mudzaone zimene zicitikako.

Ataona ponse pa nyumba ya Idesi anati, “Ha, nyumba ya mzungu imeneyi! Nzokongola ndithu zosafana ndi nyumba zathu zakale.” Anali otopa ndi ulendo wao ndipo Idesi anawakhazikitsa pampando nawapatsa madzi osulukuta nkhope kucotsa pfumbi nati, “Bapumulani, ndiphike cakudya. Abambo akabwera adzakondwa koma azizwa kuti mwayenda nokha ulendo uno wakutari.”

M'mawa mwace dotolo anabweradi nawa-nyamula kuti akamuone Ndala. Anapita pamodzi ndi Idesi ndi ana ace ena awiri. Adafika msanga kucipatala napita kucipinda komwe kunali Ndala. Asanalowemo anamva Ndala alikuceza ndi anzace nati, “Anzanga inu, ndikuuzeni! Nsomba ziri kwa Ambuyanga, kukula kwao kosaneneka, zinsomba zabasi. Kumenekonso kuli ng'ona ndi

mvuu koma ine ndinalibe konse mantha.” Ambuyace pakumva mauwo anaseka :— “Hede! mwanyo alankhula phwete ndithu!” Anampeza Ndala alikukhala pamphasa ndi ana ena awiri okhala ndi mabala pamiyendo, analikusewera ndi zithunzithunzi za mu nyusipepa (newspaper) nazidula ndi isezi (scissors). Kusangalala kwace powaona akulu acewo ! Adotolo anawasiya napita kuyendera odwala ena koma anauza mmodzi wa athandizi ace awasonyeze akuluwo zonse zakucipatala.

Anazunguliraponseponse naona zipinda zogonamo odwala, zina za amuna, zina za akazi, zonse zanya ! zosamalidwa bwino, mabedi ali ndandanda ! Anaona kucikuta kumene kubadwa ana ndiponso kucipinda kumene anacula dzinalace ‘theatre’ ndi kumene aciritisa anthu ndi mpeni pocitapo opereshoni (operation).

Atayendera cipatala conse anapita ku nyumba ya dotolo kumene anawapatsa tii ndi makeke acizungu. Bambo wa Idesi anamudandaulira dotolo kuti amuciritse nthenda ya msana nati pamsana pamamuphweteka masiku onse koma kuti pena ndi kukalamba kokha. Dotolo anati, Zoona, munthu akakalamba amva pamsana kawiri-kawiri. Anakhala naceza zambiri za miyambo yao yakale ndi mankhwala akale nafunsa za mankhwala atsopano ndi maciritsidwe a nthenda kucipatala.

Amai a Idesi analawa tii nati suga yaperewera, nanong’onezera mwana wace kuti, Suga mulibe ! Dotolo anamva nati, Kani suga yaperewera. Tengani yina. Amai anatapa masupuni awiri natakasira-takasira nkhwe-nkhwe mukapu nalawa napeza yotsekemera ndithu. Dotolo anatamanda akuluwo maleredwe ao a mwana wao

Idesi nati, "Iye ndi Mateyu anafika kuno alendo koma tsopano ali ngati abale athu akale. Ali akhama panchito nathandiza anthu ambiri. Citsanzo cao panyumba ndi pabanja ndi pamudzi ndi citsanzo ceniceni coona cacikristu. Amaphunzitsa anthu kuti ayenera kucita iwo eni zinthu zatsopano osadikirira ena awacitire. Ciphunzitso coteru cithangata anthu koposa kuwagawira cuma. Cuma angagawe ciperewera koma nzeru izi zitengera mwini cuma ceniceni cosaonongeka."

Popendeka dzuwa dotolo anapita nawo kumudzi mugalimoto nati popita masiku abwera naye Ndala kumuika kwao. Anthu onse akumudzi anacezetsa bwino alendowo nawauza kuti ana ao anali acibwenzi kwa onse. Bambo wa Idesi anamuza mkazace, "Koma ndithu mwana wathu watipatsa ulemu kuno kwa alendo. Indedi, zikomo kuti munaumirira kale kumutuma kusu-kulu, kumene anaphunzira zabwino zonsezi. Samadzikuza koma atilemekeza ife makolo ace pamaso pa anthu."

Ndala atabwera kucipatala Ambuyace anakonza ulendo wao wopitanso kwao kunyanja. Mateyu anawaperekeza kufikira kumudzi kwao pokhala anakalamba nabweranso m'mawa mwace.

Idesi ndi Mateyu nkhani yao njomweyi. Moyo wao wonse anatumikira anzao ndi mtima wakukonda ndipo mbiri ya ulemu wao inafalaponseponse. Dr. Aggrey uja wa ku West Africa anati:— "Ukaphunzitsa mkazi, waphunzitsa banja." Inde, anzanga, nzoona.

KWA AWERENGI

*Okonda kuwerenga mabuku ndikutola nzeru za
mitundu-mitundu ayenera kugula mabuku enawa
olembedwa m'Cinyanja*

NTHANU ZINA ZA AFRICAN OMVEKA

OYENDERA AFRICA

ZOMERA NDI ZOLENGEDWA ZINA

KALULU NDI NYAMA ZINZACE

NCHOWA

NKHANI YA IDESI

ARITHMETIC MAPHUNZIRO NDI MAFUNSO

AKUWERENGERA

Book I

Book II

Book III



LONGMANS